


KUWUKIRIDWA KWA UNITED STATES

 ...chifuniro cha Ambuye kuti zinthu zina zichitike nthawizina. Ife tinapita ku Denver, posachedwa pomwepa, ndipo tabwererako. Ine ndikukhulupirira iwo akufuna kufotokoza, msonkhanowo. Iwo unali umodzi wa misonkhano yabwino kwambiri imene ine ndakhalapo nayo mu zaka. Ife tinali ndi nthawi yopambana. Chinachake kupitirira pang'ono zikwi ziwiri anapereka mitima yawo kwa Khristu, pambali pa iwo amene analandira ubatizo wa Mzimu Woyera, pambali pa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zimene Ambuye wathu Yesu wokonedwa anachita pakati pa anthu uko mu Denver. Iwo anali nako kutsanulira kopambana, ndi kudza kwapamodzi kwakukulu kwa anthu. Ife tinayamba ndi pafupi zikwi zisanu, kuyamba nawo. Ndipo ife tinali ndi Mammoth Gardens. Ndipo pa usiku wachitatu, uko kunalibe ngakhale malo aliwonse a anthu kuti ayime mu malowo. Tinali ndi nthawi yodabwitsa chotero, ya mausiku asanuwo!

² Ife tinachoka kumeneko, kuti tipite ku Canada, mnyamata ndi ine. Ndipo ife tinafika pamwamba mu mapiri, ndipo kunabwera mkuntho wa chisanu. Ine ndikuganiza inu mwamva za iwo, pa wailesi zanu. Ndipo anthu ena zana ndi makumi asanu ndi atatu mphambu asanu ndi atatu anawonongeka mu iwo. Ndipo ife tinatsekerezedwa mu kusuntha kwa chisanu kwa—kwa masiku angapo, pamwamba apo mu mapiri. Ndipo msonkhano wathu unadutsa, ndipo ife tinabwerera kunyumba tsopano ife tisanati tichokenso. Kotero ife tikukhulupirira zonse izo zinali mwinamwake kwa chifuniro cha Mulungu, kuti iwo udzakhala msonkhano wabwinoko, ndi chinachakenso. Iye anali atafolitsa chinachake kwa ife chimene ife sitikuchidziwa.

³ Ife tikukhala ngati tikuyenda mdziko la mdima, koma osati mu mdima. Ife tikungotsatira pamene Kuwala kukupita, ndiye ife tikutsatira Kuwalako.

⁴ Ndipo Atate athu Akumwamba mwinamwake anali ndi chinachake chimene ife sitikudziwa kanthu za icho. Uko mwina kukanakhala kuli chowopsya china chiri kumeneko. Kapena, aponso, Iye mwina akhoza kuti amagwira ntchito pa winawake kuti amubweretse. Inu mukuona, Mulungu akhoza basi kugwira ntchito pa munthu mmodzi monga choncho; Iye amasintha fuko lonse basi chifukwa cha munthu mmodzi ameneyo, kuti awatengere iwo mkati. Ndipo kotero ife tikudziwa izo zonse zinali kwa ulemerero wabwino wa Mulungu. Ndipo ife

tikumuthokoza Iye chifukwa cha izo, ndi chifukwa chotitetezera ife. Ndipo uko kunali ochuluka ife . . .

⁵ Billy ndi ine tinathandiza kuwanyamula iwo, mu msewu monse ndi zinthu monga choncho, za anthu amene anagundidwa ndi chirichonse. Koma ife tinapyolamo popanda vuto lirilonse. Ife tinasiya msewu kamodzi, koma uko kunali chabe kwa mphindi zochepa. Ndipo munthu wina pamwamba apo, ku malo owetera zinyama anabwera pamenepo ndi kutikoka ife ndi thirakitara. Kumangoterera; iko kunali koterera kwambiri.

⁶ Ndipo icho chinali chimodzi cha zinthu zimene iwo sanakhale nacho kwa . . . Sakanakhoza, a nthawi-zakale samakhoza kukumbukira za kukhala konse ndi mkuntho ngati umenewo, mu dziko limenelo, pa nthawi imeneyo ya chaka, ku Roundup, Montana. Ndipo ife tinali . . . Ife tikudziwa kuti chirichonse chapadera kwenikweni ngati icho, Ambuye wathu anali ndi dzanja Lawo mmenemo penapake. Izo zinali kwa cholinga china, kwa—kwa ubwino wathu. Kwa ubwino wathu, ndicho chimene icho chinali.

⁷ Ndipo kotero ine ndinamuimbira M'bale Neville, nditatha ine kubwererako, ndipo ine ndinati, “Ine ndikhala ndiri kunyumba Lamlungu. Ndipo—ndipo ngati inu mungafune kuti ine ndibwere uko ndipo mwinamwake kukhala ndi Sande sukulu, bwanji, chabwino.” Ndipo ine ndinati, “Ndiye ine ndidza . . . ndipo ine ndidzakhala wokondwa kwambiri kufika potero.”

⁸ Iye anati, “Bwanji, zedi, M'bale Bill.” Anati, “Ife nthawizonse timakhala okondwa kuti inu mubwere,” ndi mtima wawukulu wotseguka ndi kukulandira, monga choncho. Ndipo anaika izo pa purogramu yake ya pa wailesi, dzulo. Kotero ife tiri oyamikira chifukwa cha zinthu zonse izi.

⁹ Ndipo mmawa uno, tsopano, pokhala Tsiku la Anakubala. Anthu ambiri, inu mumva maulaliki a Tsiku la Anakubala paliponse, ndipo anthu akuyankhula za anakubala, chimene ine ndikuganiza ndi chodabwitsa. Tisiyira izo kwa msonkhano wonsewu.

¹⁰ Mmawa uno ine ndinali nditalengeza, kuti, p—phunziro la: *Kuwukiridwa Kwa United States*, limene ine ndima funa kuyankhulapo. Chimene, inu mwinamwake munamva kulengeza kwa wailesi yanu, ndipo inu mumvetsera ochuluka a iwo lero. Ndipo apo pakhala ulaliki wa Tsiku la Anakubala, mwinamwake, usikuuno mu misonkhano. Ndipo kotero ine ndinaganiza, mmawa uno, ine ndilengeza, “ku—kuwukiridwa.”

¹¹ Ine ndinayankhula pa iwo mu Denver, kuno, osati chimodzimidzi kuchokera ku mafikidwe amene ine ndikulunga kuwupereka iwo mmawa uno, ngati Mulungu alola. Ndipo, iwo, tinali ndi nthawi yodabwitsa ndi iwo. Ambuye basi

anatalalitsa mwa njira yodabwitsa. Izo zimakhala ngati nthawizina zimatipatsa ife. . .

¹² Iwe umayenera kugwedezedwa basi pang’ono chabe, kuti uzindikire chomwe izo ziri, sichoncho ife, nthawizina? Ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu achita zimenezo.

¹³ Ndipo, tiri pomwepo, pamwamba apo, pamene ife tinatsirizira. . . Amuna a Malonda aku Denver anali amene anathandizira msonkhanowo, ndipo iko kunali kuthandizira kosiyana ndi kumene ine ndinakhalapo nako kale.

¹⁴ Ndipo kawirikawiri, atumiki, pamene iwo athandizira msonkhano, iwo amati. . . “Kodi inu munaulengeza iwo?” “Inde, kwa mpingo.” Ndizo basi za iwo. Ndiwo azibusa; iwo amafuna nkhosa zawo kuti zidziwe za iwo. Ndiyo basi. . . Ndiyo ntchito yawo.

¹⁵ Koma Amuna Amalonda anali osiyana pang’ono. Iwo ankafuna kuti dziko lidziwe za izo, kotero iwo anangoponyeramo pafupi madola zikwi zitatu kapena zinai mtengo wa kulengezera pa magalimoto onse a mumsewu, magalimoto atakisi, mabampala onse a magalimoto, ndi paliponse. Ife tinali ndi nthawi yodabwitsa.

¹⁶ Utatha msonkhano, iwo anandiyitanira ine kumbali imodzi, anati, “M’bale Branham, kodi ife tingakhoze kukuchitirani inu chiyani tsopano? Ife tiri nanu ngongole yotani?”

¹⁷ Ine ndinati, “Bwanji, zedi, palibe.” Ine ndinati, “Inu mulibe nane ngongole.” Ine ndinati, “Inu mukhoza kulipira ndalama zanga za ku hotelo, kumusi kuno, ngati inu mukufuna kutero.”

¹⁸ “O, ife tikufuna kuti tichite chinachake kwa inu.” Ndipo iwo sakanati. . . ine sindikanatenga kanthu kuchokera kwa iwo.

¹⁹ Kotero manenjala anawaitanira iwo kuseri. Iye anati, “Ine ndikukhulupirira iye amakhala ngati amakonda kusaka ndi kuweza, sichoncho iye?”

Anati, “Inde.”

²⁰ Kotero mmodzi wa amuna a malonda anali ndi kowetera zinyama kumeneko, ndipo iye anati, “Ine ndingomupangira iye chopereka cha zimenezo.”

²¹ Chabwino, Bambo Moore anapita uko kukawawona iwo, ndipo iye amayenera kubwerera pafupi mailosi makumi atatu ndi asanu, pa nsana wa kavalo. Ine ndinati. . . Bambo Moore anati, “Ine ndikanakonda kumuwona Mlongo Branham atakhala pa kavalo, akubwerera kumeneko.” Kotero iye, iwo, ndi. . .

²² Koma, zitatha izo, ngakhale, iwo anapita cha uko ku malo a nyumba ya kumunda ku Silver Plume, Colorado. Uku kukuyenera kukhala ku mbali iyi tsopano. Ndipo iwo anagula kowetera zinyama kwakung’ono cha kumeneko, ndi kundiyikirako ine nyumba ya zipinda-zisanu kumeneko

tsopano, inenso, ku Silver Plume, Colorado, pamene pali mu mtima umene wa mapiri. Kotero, inu asodzi, ine ndikuganiza ndiyo nthawi yabwino, kotero iwo akhala malo abwino kukatakasuka, ndipo pamene itatha misonkhano ndi zinthu, ngati Mulungu alola. Ndizo za kwa Iye, inu mukuona.

²³ Ine ndikukhumba tsopano kukokera tcheru chathu ku Mawu. Ndipo ine ndimangowakonda Mawu, Mawu amoyo a Mulungu. Ndizo, mkati mwa Mawu muli Moyo. Tsopano, “Mawu, lemba, limapha, koma Mzimu umapatsa Moyo.” Ndipo Moyo uli mu Mawu, chifukwa ndi Mawu a Mulungu. Moyo umakhala mu Mawu Ake.

Monga ngati ine nditakuuzani inu, “Ine ndikukupatsani inu. . .”

²⁴ Inu mukuti, “Ndine wanjala, mmawa uno, M’bale Branham. Kodi inu mungandipatse ine madola asanu?”

²⁵ Ine ndikanati, “Ine nditero.” Tsopano muli basi moyo wochulukana mmenemo monga uliri mu lonjezo langa.

²⁶ Ndiyo njira yomweyo izo ziliri ndi Mulungu. Pamene Mulungu alonjeza chirichonse, ndiye chimene Mulungu ali, Chake. . . Iye ayenera kukhala mu Mawu Ake. Mwaona? Mawu awa ali oyenera ayi. . . Mawu awa ali basi ofanana ngati Mulungu. Iwo ali Mulungu.

²⁷ Mawu ako ndi chimene iwe uli. Ndilo lumbiroo lako; ife tinkalitcha ilo. Chokumanga chako ndi mawu ako. Ngati ife sitingakhoze kutenga mawu ako, ndiye ine sindingakhoze kukhala nacho chidaliro. Koma ngati ine ndingakhoze kutenga mawu ako kwa chirichonse, ndiye ndi munthu wa chilemekezo.

²⁸ Ndipo Baibulo linati, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.” Mwaona? Mwaona? “Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndi kukhala pakati pathu.”

²⁹ Ngati ife tingaganize, ndilo dziko lapansi lomweli limene ife tikukhalapo, mmawa uno, ndi Mawu a Mulungu. Mtengo *uwo* ndi Mawu a Mulungu. Ndipo inu, thupi lanu, ndi Mawu a Mulungu. Mulungu analiyankhula ilo kuti likhalepo monga choncho, kulipanga ilo kuchokera kopanda kanthu; limene linalibe kanthu.

³⁰ Kodi inu munayamba mwazindikirapo moyo wa munthu, kumene iwo unachokerako? Khungu limodzi laling’ono, lochepa kwambiri mwakuti diso laumunthu silikanakhoza kuliwona ilo; kokha kupyolera mu galasi lalikulu, lamphamvu. Ndipo kuchokera mwa ilo kunabwera munthu wa mapaundi zana-ndi-makumi asanu, mazana awiri. Kodi ilo linabwera kuchokera kuti? Mwaona? Mulungu anangoyankhula ilo, ndipo ilo linangoyamba, mwa chirengedwe, kumakula, ndipo apo ilo linabala chimodzimidzi basi. Iye anayankhula mtengo uliwonse,

chirichonse, kuti chikhalepo. Ndipo ndicho chodabwitsa chotero, chinthu chodabwitsa, mmawa uno, kuwapenya Mawu a Mulungu.

³¹ Tsopano ichi, mmawa uno, mu Chipangano Chakale, kutembenezira cha ku Mbiri. Ine ndakhala ngati nditasokonezedwa pang'ono... Pamene inu mukutembenezira tsopano ku Mbiri, mutu wa 18. Wotopa pang'ono chabe. Koma ngati Ambuye alola...

³² Ine sindiri wotsimikiza; ife tidzadziwa zochuluka Lachitatu usiku. Ngati Ambuye alola, ndipo mpingo ukamverera kutsogozedwa mwa njira imeneyo, ine ndikanakondwa kukhala ndi Lachitatu, Lachinai, Lachisanu, Loweruka, ndi Lamlungu, ngati chitsitsimutso pano, chitsitsimutso chophunzitsa chabe kuchokera ku Mawu. [Osonkhana, "Ameni."—Mkonzi.] Lachitatu, Lachinai, Lachisanu, Loweruka, ndi Lamlungu, kuphunzitsa chabe pa Mawu; osati misonkhano ya machiritso, koma kuphunzitsa. Mwinamwake Ambuye atitsogolera ife mnjira imeneyo. Ndiyeno ife... Ine ndimangokonda kukhala ndi inu ndi kukhala nacho chiyanjano pozungulira Mawu, ndi inu. Zikomo inu, mochuluka kwambiri, chifukwa cha "ameni." wabwino, wodabwitsa.

³³ Tsopano mu mutu wa 18 wa Mbiri, ndi kuyambira ndi ndime ya 12, ife tikufuna kukhazikitsa malingaliro athu, basi kwa kanthawi pang'ono pa phunziro lopambana ili la tsikuli. Mbiri Yoyamba... Kapena, Mbiri Yachiwiri, ine ndikupempha kukhululukira kwanu. Mbiri Yachiwiri 18:12, ndipo ife tiwerenga gawo la iwo pano, ndipo tiwone chimene Ambuye athu ati akhale nacho kuti ife tidziwe.

Ndipo mthenga amene anapita kukaitana Mikaya ananena kwa iye, kuti, Taonani, mawu a aneneri anenera chokoma kwa mfumu ndi kuvomereza kumodzi; mulole mawu anu chotero, ine ndikukupemphani inu, akhaletu ngati amodzi a iwowo, ndipo muyankhule inu chokoma.

Ndipo Mikaya anati, Pali YEHOVA wamoyo, ngakhale chimene Mulungu wanga anena, chimenecho ine ndidzayankhula.

Ndipo pamene iye anafika kwa mfumu, mfumu inanena kwa iye, Mikaya, kodi ife timuke ku Ramotigileadi ku nkondo, kapena ife tileke? Ndipo iye anati, Kwerani inu uko, ndipo mukapambane, ndipo iwo adzaperekedwa ku dzanja lanu.

³⁴ Tsopano kuti tikhazikitse lingaliro lathu kwa mphindi zochepe; liwu limodzi chabe kwa Iye kachiwiri, pa izi.

³⁵ Atate athu Akumwamba, ndi mitima yoyamikira ife tikukuyandikirani Inu basi tsopano, mmalo mwa miyoyo yotayika, mmalo mwa iwo amene ali osowa, mmalo mwa mpingo.

Pa...Mulole Mzimu Woyera ulowe mu Mawu mwamsanga tsopano, ife tikupemphera. Kuwatengera Iwo molunjika kumene ku mtima uliwonse pano umene uli ndi chosowa. Ndipo pamene Iye azipereka Uthenga Wake wa mphamvu ya Mawu kupita mu mtima, mulole ife tonse tipambane mwa Iwo, mmawa uno; kumapita, kuchokapo pa kachisi, tikusangalala ndi kutamanda Mulungu, tikunena, “Mitima yathu ikutentha mkati mwathu chifukwa cha Kukhalapo Kwake.” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

³⁶ Choyang’anapo chathu chikukhazikitsa, mmawa uno, pa chachisoni. Ndipo Chipangano Chakale, kwa ine, chiri nthawizonse mthunzi kapena—kapena kulosera kwa Chipangano Chatsopano. Nthawi zambiri, winawake wanena, “M’bale Branham, nchifukwa chiyani kuti inu nthawizonse mumatenga Chipangano Chakale? Pafupifupi nthawizonse, kutenga mutu, inu nkubwerera nawo ku Chipangano Chakale.” Ine ndimachita izo chifukwa ine ndimakonda kufanizitsa. Ine ndimakonda... .

³⁷ Maphunziro anga ndi operewera kwambiri, monga nonse mumadziwa. Ndipo njira yokha imene ine ndimayidziwa yokhalira penapake pafupi ndi cholondola, ndi kuwona chimene pateni inali, kuyang’ana pa chojambulidwa ndi kuwona chimene icho chinali. Ndiyeno ine ndimadziwa chimene *icho* chinali chidzakhala chinachake chofanana kwa chimene *ichi* chiri pano, chifukwa ndiwo mthunzi chabe wa icho. Ndipo ine nthawizonse ndimayang’ana mmbuyo ku Chipangano Chakale kuti ndiwone chimene ana a Israeli anachita, kuwona chimene chilango cha tchimo chinali, kuwona chimene chilungamo cha aneneri chinali, kuwona zomwe zinthu zonse izo zinali; ndiyeno ine ndimakhala nalo lingaliro chimene *ichi* chiri pano, chimene chaonetsedweratu chimene chiti chidzakhale mu kutsirizitsa wamba kwa pa mapeto.

³⁸ Pa nthawi iyi, apo nkuti panali chinthu chachikulu chikuchitika kwa Israeli. Izo zinali mu mdima wandiweyani wa pakatipausiku pake.

³⁹ Mu Chipangano Chakale, ngati Ambuye alola, mwinamwake mu misonkhano ikudzayo, ine ndikufuna kuti ndiwonetse momwe kuti Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo inafanizitsidwira mu Chipangano Chakale. Momwe kuti iwo anayambira chimodzimodzi basi monga pa—kuyamba kwa Mibadwo ya Mpingo ya mpingo wa Amitundu, ndipo anapita kumene mmusi kupyola mu m’badwo wa mdima wofanana, ndi kutulukamo kulowa mu nthawi yaulemerero ya Pentekoste, pa kugwa kwa Mzimu Woyera mu mpingo woyambirira wa... .mu m’badwo wa Chiyuda. Ndiye kupita kupyola mu nthawi ina ya mpingo wa Amitundu, kupyola mu m’badwo wa mdima, ndiyeno kutulukiranso mu Zakachikwi, pa mapeto.

⁴⁰ Tsopano, momwe kuti mmbuyo mkati mwa zakazana kumeneko, mfumu yaikulu iyi Ahabu inakwera mu mphamvu. Ndipo iye anali ngati amakwera pa mbiri ya mafumu ena a Chiisraeli, amene anali. . . Ahabu, iyemwini, anali ngati wo—wokhulupirira wa mmalire. Ine kawirikawiri ndafanizira kwa iye mwa njira imeneyo, chifukwa iye anali gawo la nthawi ku mbali *iyi* ya mpanda, gawo la nthawi ku mbali *iyoy* ya mpanda.

⁴¹ Iwe sungadziwe poti umuyimike, munthu amene ali wosakhazikika monga choncho. Kapena, munthu yemwe amadzinenera kuti ndi Mkhristu, ndipo kusakhazikika kumeneko, iwe sumadziwa choti uchite ndi munthu ameneyo. Lero iwo ndi Akhristu; mawa iwe sukudziwa pamene iwo ali. Mu mpingo lero, iwo akusangalala ndi kumaimba ndi kutamanda Mulungu; ndipo mawa, kunja akumwa, kuphokosera, kumathamangathamanga. Ndiye munthu wa mtundu umenewo ndi wovuta kuti ungachite naye chirichonse.

⁴² Ine ndikukumbukira, ndiri mnyamata, kamodzi ife tinali—tinali ndi kavalo wokalamba, amene anakonda kumalumpha mipanda nthawi zonse. Ndipo ine ndikuganiza ambiri a inu anthu, pa usinkhu wangawu, mungadziwe kale mu masiku a kavalo, masiku a ngolo. Ine ndabwera nthawi zochuluka, mpaka mmusi mu msewu uwu kuno, ndikuyendetsa kavalo ndi ngolo, inemwini. Ine ndiri makumi anai ndi zisanu. Kotero, iwo, nkukumbukira. . . Kavalo wakale uyu, ife tinkayika goli pa khosi lake, monga inu mungachitire ng’ombe, ndi kumuletsa iye kuti asamalumphe mpanda. Ndipo iye ankalumpha, mulimonse. Ndipo iye amakhoza kupachika goli ilo ndi kumutembenezira iye pamenepo, ndi zina zotero. Iye amawulumpha mpandawo. Ndipo tsiku lina, chimene iye. . .

⁴³ Ine ndinkadabwa chimene chinali kudolola kanthu kakaleko. Ndipo apo panali dzenje lakuya lakale pansu pamenepo. Tsopano iye anali kuyima mu msipu, wautali, koma iye ankafuna. . . Apo panali masamba ena a udzu wa pa mtengo wa zipatso mu dzenje lakuya. Ndipo iye ankalumpha mpanda umenewo ndipo ankalowa mu dzenje lakuya limenelo mmene mawayi onse awa ndi galasi. Chabwino, iye anali mwathu—motayira mwathu, ndipo kupita mmenemo kuti akapeze zodzadza mkamwa pang’ono za udzu wa mu mitengo ya zipatso. Ndipo ife tinkachita kukatenga akavalo ena ochuluka ndi kumukoka iye kuchokera mu dzenje lakuya ilo. Pamene iye anafika mmenemo, iye anakodwa mmwamba. Ndipo pamene iye anaima panja pamenepo, iye anali akunjenjamera ndi kuwukha magari, ndi—ndi momwe iye analiri, basi kuti akapeze zodzadza mkamwa, kapena kawiri, za udzu wa mitengo ya zipatso uwo, pamene iye anali kuima mu msipu, pafupifupi kufika mu maondo ake.

⁴⁴ Ine kawirikawiri ndalingalira za chithunzi chimenecho. “Njira ya wochima ndi yovuta.” Iye sangakhoze basi kukhala

chete pamene iye anali kumadya ndi kumakhala ndi nthawi yodabwitsa, koma . . . iye anachita kulumpha mpanda ndi kupita kukavulazidwa yense ndi kuchekedwa monga choncho, basi kuti akapeze udzu wodzazamkamwa wa—wa mtundu wina wosiyana. Tsopano ndiyo basi pafupifupi njira yomwe anthu amachitira, amene amalumpho mpanda wa msipu wa Mulungu. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Kupita kunja, kupita kunja; kubwera mkati. Ali mu mpingo, akukhala nayo nthawi yodabwitsa; ndiye, mawa, kukadzigulitsa kunja kutsata chinachake chonga icho. Izo zimapangitsa izo kuvuta kwambiri.

⁴⁵ Ahabu anali mochuluka kapena mochepea munthu wa mtundu umenewo. Mbali iliyonse mphepo inkawombera, Ahabu amakhala nkhami ziri zokonzeka, ngati iko kunali mbali *iyi* kapena mbali *iyi*. Chikwati chake chinamufikitsa iye yense mosokonezeka, ndi mkazi wamng’ono yemwe anali kalonga wamkazi wamng’ono, mwana wamkazi wa mfumu, Yezebeli. Wokongola kwambiri kuti umuyang’ane, mkazi wokongola kwambiri, koma mu mtima mwake iye anali mthakati. Ndipo iye anali wamafano, ndipo iye anapangitsa Israeli yense . . .

⁴⁶ Tsopano, momwe ine ndikanafunira kuzungulira pamenepo basi kwa maminiti ochepea, tinali, tiri kufika pachimake pa izi pa umayi, onani, pamenepo. Ndipo pamene munthu ayamba kuti akwatire; mtundu wa msungwana, mkazi yemwe iye . . . Ndi zochulukira kuposa kungoyang’ana pa kukongola. Iwe uyenera kumupeza winawake, zonse moyo ndi thupi nzolumikizana limodzi; winawake yemwe kwenikweni ati akhale mzako ndi bwanawe, yemwe ati adzamamatirane ndi iwe kupyola mu zokandapala ndi zopyapyala.

⁴⁷ Tsopano, koma, Ahabu, iye anangotengeka naye chifukwa iye anali wokongola, ine ndikuganiza, ndi kumukwatira. Icho sichikanakhoza kukhala china chirichonse za iye, chifukwa mthakati monga iye analiri. Ndipo iye anabwera kumeneko. Ndiyeno, ndithudi, pokhala atakutidwa ndi iye monga chomwecho, ndi kumukonda iye, bwanji, iye anapangitsa Israeli yense kuti achimwe ndi kuti apite motsutsana ndi Mulungu, ndi kugwetsera pansu maguwa a Mulungu; kumanga maguwa a Baalimu. Ndipo iwo anali nako kupembedza kwa Baala monse mu Israeli yense, pa nthawiyo.

⁴⁸ Tsopano, mkazi wake anali atapangitsa Naboti wolungama . . . Ambiri a inu mwawerenga za iye. Momwe iye anatengera munda wake, mwa chinyengo; ndipo analumbira, bodza, ndipo anali nazo mboni zabodza momutsutsa iye. Chifukwa, iye ankafuna kumuchitira chinachake mwamuna wake; ndipo anapha munthu wolungama, polinga kuti atenge munda umene unalumikizana mwapafupi ku malo a nyumba yachifumu.

49 Zonse izi, Mulungu anali kuyang'ana pansi. Kotero mneneri, Eliya, amene anali wamkulu, wantchito wamphamvu wa Ambuye, analosera ndipo anamuuzza Yezebeli chimene chikanati chidzachitike kwa iye. Ndipo iye anamuuzza Ahabu kuti agalu akanadzanyambita magazi ake omwe. Tsopano, pamene Mulungu wanena chirichonse. . . Zedi, masiku amenewo, Mawu olunjika a Ambuye ankadza kupyolera mwa mneneri.

50 “Mulungu, mu nthawi zakale ndi manenedwe osiyana ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri, mu tsiku lotsiriza ili kupyolera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.”

51 Kotero, *Awa* ndi Mawu. Ndipo ngati chirichonse chiri chosiyana kwa Amenewo, chisiyeni icho chokha. Mwaona? Tsopano, mwachiwiri, Iye akuyankhula lero kupyolera mwa mneneri, mpenyi, ndi zina zotero. Koma poyamba ndi *Ichi*, Mawu, tsopano.

52 Ndipo Ahabu anali atachita uthakati uwu. Ndipo iye anapitirirabe: Mulungu akudalitsa anthu kwa zaka zambiri. Ndipo, potsiriza, Yehosafati anali mfumu ya pa Yuda, pamene Ahabu anali mfumu ya pa Israeli.

53 Ndipo, ndiye, Yehosafati anali munthu wolungama. Iye anali mwana wamwamuna wa Asa. Asa anali m—munthu wolungama, ndipo iye anagwetsera pansi maguwa onse a— a mafano; anamanganso maguwa a Yehova. Ndipo iwo anali ndi—ndi chitsitsimutso, monga izo zinali, kumeneko mu Yuda. Ndiyeno patapita kanthawi, Yehosafati kapena. . .

54 Ahabu, kani, anatumiza uko, ndipo iye anapeza chigawo china cha dziko, mu Siriya, amene iye ankaganiza kuti anali a iye, amene iye ankaganiza kuti iye apita kukawatenga. Kotero iye anamufunsa izi Yehosafati ngati iye akanabwera ndi kupanga chigwirizano ndi iye.

55 Ndipo, ndithudi, apo pali changozi chachikulu tsopano, onani, pamene iwo anayiwona mfumu yayikulu iyi, Ahabu, kumene kuja, ndipo iwo anawona wamkulu uyu akubwera apa, Yehosafati; mmodzi wa iwo, wofunda; winayo, munthu wodzazidwa—Mzimu. Penyani momwe inu mumapangira chigwirizano chanu. Penyani chimene inu mukuchita, momwe inu mumadzimangirira nokha ndi osakhulupirira. Dzisungeni nokha oyera, makamaka mu tsiku limene ife tikukhalamo.

56 Ine ndikukhulupirira, mpingo, popanda mthunzi wa kukayika, ichi chawotcha pa mtima wanga. Ndicho chifukwa ine ndikuyang'anira mausiku asanu awa, posachedwapa; kuti kamodzi kenanso, izo zisanachitike, tiwupatse mpingo uwu kupesa kwabwino, kupyola mu Baibulo.

57 Ife tikukhala mu mithunzi ya nthawi. Izo zikhoza kuchitika nthawi iliyonse. Pamene ife tiwona nthawi zikubwera kuti zinthu zichitike; uthakati umene wa mdani, mphamvu zimene. Ife tikuyang'ana pa mikuntho ya chisanu iyi ndi chirichonse

chikuchitika, zowawitsa zonse izi, zinthu zonse zosiyana. Ndizo zonse zinapangidwa ndi kusokonezeka uku, kwa kuwombera mabomba awa ndi zinthu. Iwo akupangitsa zinthu zonse kusokonezeka kuno. Ndipo iwo akusokoneza mu laboratore yayikulu ya Mulungu, kuti akwaniritse Mawu Ake. Izo zifika pochitika.

⁵⁸ Koteru, “mwamuna wa tchimo” akuwuka, mphamvu, mwachinyengo kwambiri. Mai! Ine ndinamumva mlaliki mmawa uno, mwamuna wodzazidwa-Mzimu, akutenga chilemba cha chilombo ndi kumanena kuti wotsutsakhristu anali Russia. Ndi kulakwitsa kotani! A-nha! Russia alibe kanthu kochita ndi icho. Ayi, bwana. Ndizo Mwamalemba. Tsopano, koma zindikirani mu nthawi yopambana iyi imene ife tikukhalamo, chenjezo.

⁵⁹ Tsopano, Yehosafati uyu, akumverera kukhala ngati mwabwino chifukwa mfumu yayikulu ya Israeli inati, “Bwera, udzandichezere ine.” Ndipo iye anapita kumeneko. Ndipo iwo anatenga ng’ombe ndi nkhosa, ndi zina zotero, anachita nsembe. Nthawi yonse, mu mtima mwa Ahabu pansi mmenemo, iye anali wachinyengo, chifukwa iye sanali kupembedza Chimenecho, kapena kupereka nkhosa izo ndi zinthu ndi mtima wona, chifukwa, kuwonjezera apo, iye ankatsamira kwambiri ku chipembedzo cha mkazi wake.

⁶⁰ Ndipo zindikirani, basi monga Ahabu anakwatira Yezebeli mu nthawi ya m’badwo wawukulu wa mdima uwo wa Israeli, iye anabweretsa kupembedza mafano mu Israeli, choyimira kumene cha lero. Basi mu m’badwo wa mdima; pamene ife tinatuluka kupyolera mwa atumwi oyambirira, kubwera kwachiwiri, kubwera kwachitatu, mpaka mu m’badwo wa mdima, zaka mazana khumi ndi asanu. Basi monga Ahabu anakwatira Yezebeli ndipo anabweretsa kupembedza mafano mu Israeli, chotero unachitanso mpingo wa Mzimu Woyera kukwatira mu ziganizo, ndi kupangitsa kupembedza mafano kubweramonso, ndipo lero ndiwo mawonekedwe a Chikhristu. Mwaona? Onani, mdima wambiri basi! Ndipo tsopano izo zasunthira mpaka pansi, tsiku lirilonse; m’badwo wa mpingo uliwonse ukusunthira pansi ku chinthu chomwecho, ku chimake chachikulu, chikhaliidwe chofunda, chikubwera, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya wofunda! O, ndi nthawi yoyipa chotani imene ife tikukhalamo!

⁶¹ Mvetserani. Ine ndikufuna kuvomereza pakali pano, ine ndisanapite mopitiriza mulimonse. Ine ndine mlaliki wachikale yemwe ndakhala ndikuyembekezera kuti ndiwawone masiku akale kachiwiri. Ine ndawona zochuluka kwambiri za kutsanzira uku, Hollywood kukongoletsa Uthenga, mpaka ine ndiri wodwala kwambiri ndi wotopa nazo. Inde, bwana. Ine ndikufuna kuwona kwa kachitidwe kachikale. Ine ndikuwopa ife tikupanga Chikhristu chokongola kwambiri kwa anthu; mzere wangozi.

62 Tsopano Yehosafati akubwera uko, akuganiza, “O, chabwino, mfumu yayikulu iyi ya Israeli, ine basi...O, ife tidza...Izo zikhala bwino.” Ndipo mkati kumene mwa kukongola kwakukulu konse uku, kodi iye anachita chiyani? Iye anapanga ubwanawe, kuti apite uko ndi kukamumenya mdani, pa chifukwa chofanana, chifukwa iwo anati, “Ife tiri tonse anthu ofanana.” Koma iwo sanali. Wina anali gulu lodzazidwa—Mzimu, mmodzi winayo anali gulu lofunda. Iwo sali anthu ofanana. Ayi, bwana. Iwe sungakhale nako. . .

63 Mdimba sungakhoze kukhala nacho chijanano ndi kuwala. U—usiku sungakhoze kukhalapo mu kukhalapo kwa kuwala kwa dzuwa. Ndipo nthawi yachinyengo kwambiri imene ilipo ndi pakati pa nthawizo. Pamene dzuwa likulowa kumene kapena kutuluka, ndi nthawi yachinyengo kwambiri imene ilipo. Apo sipamakhala kupenya kokwanira kuti upenye bwinobwino; nyali zako pa galimoto yako sizimawonetsa bwino ndi mowala. Ndi kwabwino kuti kukhale mdimba kapena kowala. Yesu anati, “Mukhale otantha kapena ozizira, osati ofunda.” Basi, ndiwo mzere wa ngozi.

64 Ndiyeno Yehosafati, pamene iye anafika uko, ndiyeno ubwanawe waukulu uwu unapangidwa, umene sunamukondweretse Mulungu. Ndipo zindikirani, basi mu nthawi ya zake, kutengeka konse tsopano, “Ine ndakondedwa ndi mfumu iyi. Ndipo, o, ine—ine—ine ndiri ndi chijanano ndi woyandikana naye uyu. Ine ndiri. . .”

65 Onani, khalani osamala, zimenezo, mpingo! Mwaona? Ndicho chimene chimayambitsa vuto lonse kuzungulira kachisi uyu pano, ndi kuzungulira ena. Mwaona? Khalani osamala ndi chimene inu mukusakanizikana nacho. Mwaona? Tulukanimo, ndipo mwina mukhale a Khristu kapena mukhale womutsutsa Iye. Mwaona?

66 Tsopano, munthu uyu anapanga ubwanawe, ndipo iye ankaganiza kuti iye anali atachita chinachake chachikulu. Komabe, pamene iye anati, “Kodi kulibe uko tsopano, ife tisanapite kumeneko, ife tiyenera kufunsira Ambuye za izi?” Tsopano, Yehosafati anali nacho chipembedzo chokwanira chitatsalira mwa iye, mu kulakwitsa kwake, kuti iye anali atapita kumusi uko kwa mfumu iyi, koma iye anali nacho chipembedzo chokwanira chitatsalira mwa iye kuti aganize, “Chabwino, ife tiyenera komabe kufunsira kwa Ambuye.”

67 Tsopano, Ahabu anali kumapitabe wopanda kunena mawu; basi mwakukhoza kwake komwe, mwachithupi, njira ya umunthu yochitira zinthu.

68 Ine ndikungodabwa pakali pano, mpingo, ngati izo sizinakhale, nthawi zochuluka, ife tapanga kulakwitsa. Kuchilingalira icho, ndi kunena, “Chabwino, icho chiyenera

kukhala mwa njira *iyi*,” ndipo ife tazikhazikitsa izo monga chomwecho.

⁶⁹ Ine ndikuganiza ndi pamene gawo lonse la kulalikira kwa America kuli lero, kuti ife takuika iko mu mawonekedwe a—a, ine ndinganene kuti, kulalikira kwa ku Hollywood, gawo lonse la kukongola. Ife tikuzindikira alaliki amabwera ku nsanja, lero, ndipo, mai, iye ali yense wotukumuka, ndi kumanena zochulukira zonse za nthabwala iye asanayambe kulalikira, ndi zinthu monga choncho, ndi kumapitirira ndi kumachita ngati wazisudzo, mu guwa. Pamene iyo ifika nthawi kuti apange kuitanira ku guwa, anthu sawona nkomwe kuwonamtima kulikonse kopangira kuitanira pa guwa nako. Ndiko kulondola. Ndicho chifukwa dziko lalowa mu chikhaliidwe chofunda lero, chomwe ilo lirimo.

⁷⁰ Ine ndikudabwa, lero. Ziri basi, lero, ine...Mpingo, ife tikuyesa kuwatumiza anyamata athu ku sukulu, kuti akaphunzire kuweringa maganizo, ndi zina zotero monga chomwecho, kuti adziwe momwe angaperekere dongosolo, kuti azifika mu guwa ndi kulinganiza zathu...Uthenga uli wodolola kwambiri, mwakuti iwo uwagwire anthu, ndi kugwira tcheru chawo. Ndipo ambiri a owerenga maganizo aakulu amapita kunjira ngati aphunzitsi monga choncho, ndi kuchita masewero ndi kudzipangitsa zochulukira zonse za chinachake. Ndipo ine ndikungodabwa, pamene iwo...Ife nthawizonse tikuwauza iwo kukongola ndi kukopa kwa mpingo. Koma ife timalephera kuwauza iwo, “Iye amene ati anditsate Ine, mloleni iye adzikane yekha, atenge mtanda wake ndi kunditsata Ine.” Ine ndikudabwa ngati ife sitinapange kukongola kwa mpingo kokongola kwambiri, kwa munthu amene amabwera mmenemo.

⁷¹ Mwa chitsanzo, mpingo wa Baptisti lero uli nako kuyankhula, “Milioni ena mu ’44,” kutengera mkati mamembala mwa zikwi, ndi makumi a zikwi, osatembenezidwa, anthu chabe amene amalowa mkati ndi kujowina mpingo. Ndipo ndicho chobwerekera kwa Mpingo wa Yesu Khristu, kutengera mamembala otero mkati. Iwo amamwabe. Iwo amasutabe. Iwo amachitabe njuga. Iwo amanamabe.

⁷² Iwo amabwera ku mpingo, kuyembekezera kuti adzasangalatsidwe ndi gulu la alaliki aku Hollywood amene amawuka, atavala kukongola kochulukira, ndi zing’wenyeng’wenye zochulukira zazikulu zitakhala pamwambandi-mmusi pa nsanja.

⁷³ Pamene, iwo akuyenera kukhala nako kachitidwe kachikale, Mulungu-poyamba, kulirira, kuitanira pa guwa kumeneko; kumene amuna ndi akazi samabwera kuti adzakongoletse, kapena kuthamangapo ndi kuchita chitsudzo, koma kupita pansu ku guwa ndi kuzindikira kuti imfa ya Yesu Khristu apo, amene

anawafera iwo, kuti iwo akubwerera moonamtima ndi Mulungu kachiwiri.

⁷⁴ Ine ndikudabwa ngati ife sitikukhala mu nthawi ya mtundu umenewo, pamene ife timatenga alaliki aakulu, monga ambiri amene akuwoloka maiko lero, a alaliki odziwika-kwakukulu amene aphunzira kuwerenga kwa maganizo ndi kuwakopera anthu ku mpingo. Koma inu mutatha kuwatengera iwo mu mpingo, ndiye inu muchita chiyani kwa iwo? Iwo achita chiyani—chiyani atatha iwo kulowa mu mpingo? Basi kujowina mpingo, ndi kubwerera mmbuyo ndi tchimo lomwelo ndi chikhumbo chomwecho chimene iwo anabwera nacho mu mpingo. Iwo amabwerera mmbuyo mwa njira yomweyo. Ndipo ndicho chifukwa, lero, dziko limayang’ana apo, nkunena, “Chabwino, ngati munthu *ameneyo* ali ndi chipembedzo, ngati munthu *uyu* ali ndi chipembedzo. . .”

⁷⁵ Ine ndikuwopa ife tachipanga icho chophweka kwambiri. Ndicho, ine ndimakonda. . .ine ndikuganiza, chisangalalo, ndithudi, ine ndikukhulupirira kuti zisangalalo zonse zagona mwa Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Ine ndikukhulupirira ndi chisangalalo ndi kukondwa. Koma kumbukirani, m’bale, ndiyo njira ya kuwawa ndi kuvutika ndi mtanda. Inu muyenera kuzindikira zimenezo, aponso. Ndiko kulondola. Ine ndikudabwa ngati ife sitinapake utoto pang’ono aponso—pang’ono kwambiri mokhala ngati kusalaza.

⁷⁶ Ine ndinali kuyang’ana, ndipo mkazi wanga anaika. . . Timachokapo, ndipo iye anaika duwa pa chikhoto changa mmawa uno. Iye anati, “Iwe uyenera kuvala ilo. Mayi ako akanali moyo.”

Ndipo ine ndinati, “O, wokonedwa, ine sindikudziwa.”

⁷⁷ Tsiku la Anakubala ndi lodabwitsa, koma izo ndi monga dziko, iwo achipanga chinthucho mwamalonda, basi mwawamba kuti azigulitsa maluwa ndi zinthu monga choncho. Bwanji, ndi chonyozetsa kwa anakubala. Bwanji, amayi anga ndi anakubala tsiku lililonse la chaka, inde, bwana, osati tsiku limodzi chabe.

Ine ndikati, “Kodi inu mumawakonda amayi anu?”

⁷⁸ “Ine ndinawatumizira iwo nkhatu ya maluwa Tsiku la Anakubala lapitalo.” Chabwino, m’bale, iwo ayenera kukhala mayi tsiku lililonse. Koma ndi zamalonda.

⁷⁹ Duwa limenelo ndi lokongola. Ine ndimakonda duwa lokongola. Ine ndimaganiza za izo monga ngati ine ndimachitira. . .Ndi lokongola bwanji duwalo! Ilo limamasula. Ndipo ilo liri ndi fungo. Ndipo odutsapo amanunkhiza ilo. Nyama zimabwera pafupi, kuzanunkhiza ilo. Koma, tsopano penyani, ndi lokongola. Monga Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu, Ndicho chinthu chaulemerero kwambiri; machiritso Auzimu, ndi mphamvu, ndi zodabwitsa, ndi zizindikiro, ndi

zozizwitsa, ndi ufulu atachoka ku tchimo. Ndi malo okongola. Koma, onani, ngati duwa ilo...Ife tidzayenera kubwera, Mpingo, monga chirengedwe chonse.

⁸⁰ Duwa limenelo, pokhala lokongola, ng'ombe iliyonse mu dziko inganyambite pa ilo ngati iyo ingathe. Koma chirengedwe chinapereka mabenesi aang'ono, nthungo zazing'ono zitatulukira kunja uko, zotchedwa minga, ndipo izo zimawasiyitsa iwo kutali. Izo zimawateteza iwo. Ndizo chimodzimidzi.

⁸¹ Ndipo ine ndikuganiza, lero, ngati ife tiribe Mawu a Mulungu, akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, kozungulira pa kukongola kwa mphamvu ya chiyero cha Mulungu, ife tilora ng'ombe iliyonse mu dziko kunyambita pa Iwo ndi kuwathothola Iwo. Iyo idzawanyambita Iwo. Ichochidzakhala chobwerekera kwa Mpingo. Ndiko kulondola.

⁸² Ine ndikuganiza, lero, chimene ife tikusowa ndi kuchuluka kwa kachitidwe kachikale, atumiki oyitanidwa ndi Mulungu, aawisi, mwina opanda maphunziro ochuluka, koma adzawabweretsa anthu pansi ku guwa, ndipo pamenepo kuwawitsidwa. Osati ndi chimwemwe ndi kumaseka, ndi kumatafuna chingamu, ndi kuyika dzina lawo pa pepala; koma, m'bale, kulira kwachikale ndi kufa, mpakana amuna ndi akazi atalapa kwathunthu kuchoka ku machimo awo ndi kubwera pafupi kwa Mulungu. Amen.

⁸³ Ine ndikukuuzani inu, ife tiyenera, “Kwezani manja anu, amene mukufuna kumulandira Khristu,” onse monga choncho. Ndizo zonse zabwino, m'bale, koma izo siziti—izo sizimachotsa tchimo.

⁸⁴ Iwe uyenera kulapa choyamba, fika polunga, kafike pansi apo ndi kukalira kwenikweni. Ine ndikhoza kukumbukira nthawi zimene anthu a kachitidwe kachikale ankayenda pansi kupyola mu tinjira, ndipo kukwera-ndi-kutsika mmisewu, akulira, ndi kumayankhula kwa oyandikana nawo. Amenewo anali Akhristu a tsiku limenelo, kuwauza za zinthu za Ambuye.

⁸⁵ Ndipo, lero, ife timaika dzina lathu pa bukhu la mpingo, ndi kutuluka kukakhala kunyumba, ndipo osanena konse liwu za Iwo. Osakhudzidwa! “Basi malingana ngati ife tiri a mu mpingo, zonse ziri bwino.” Ine ndikutsimikiza ife tikulakwitsa pamenepo, anthu. Fufuzanipo! Pakuti, izo sizidzayima mu Ziweruzo. Ayi, bwana. Izo sizidzatero.

⁸⁶ Palibe zoperevera, “Iye amene ati anditsate Ine, msiyeni iye adzikanize yekha, anyamule mtanda wake, ndi kufa tsiku ndi tsiku.” Akhale chifereni, apo pa mtanda. Ndiko kulondola. Mowawa! “Njira, ine nditenga njira,” inu mumayimba, “ndi onyozedwa apang'ono a Ambuye.”

⁸⁷ Ine ndikuganiza lero, ndi nthawi yotani imene ife tikukhalamo! Kuti, kulalikira, iwo amakuika iko mu nyali

zowala mopambana kwakukulu, ndipo iwo amayesera... Pamene iwe uwona mlaliki akubwera ku tawoni, iwe umadabwa. Ine, misonkhano yanga yakhala yolakwa mofanana. Ndiko kulondola. Ine ndimadabwa ndi ndani akubwera ku tawoni, nthawi zina, mlaliki kapena Yesu Khristu? Bwanji, iwo ali...

⁸⁸ Ine ndinapita ku malo kuno, osati kale litali, kumene mvangeli wina amayenera kubwerako. Ndipo Dzina la Yesu... Bwanji, iwo anali ndi chithunzi cha mlaliki, “mwamuna wa ora,” mwamuna wokhala ndi *ichi*, ndi mwamuna wokhala ndi *icho*.

⁸⁹ Ine, nthawizina ine ndimaganiza za utumiki wanga, ndi kuwaona anthu akubwera. Ndipo ine ndimafika mu chipinda cha hotelo, kunena, “Mulungu, ndani—kodi anthuwa akubwera kudzamuwona ndani, ine kapena Inu?” Mwaona? “Ngati iwo akubwera kudzandiwona ine, iwo atayika, apabe; koma, O Mulungu, ndiphwasulireni ine pansi, ndichotsenipo ine. Ine ndikufuna kukuimirani Inu, Mmodzi yemwe mudzaima patsogolo pake tsikulina, ndi manja onjenjemera ndi kunjenjemera, thupi lofooka, akuyang’ana kwa Inu. Kudziwa kuti moyo wanga wapachikika pa kusankha Kwanu.” Tiyeni ife timukweze Khristu.

⁹⁰ Lero, inu mukuti, “Chabwino, ine ndine wa Baptisti. Ine ndine wa Methodisti. Ine ndine wa ku kachisi. Ine ndimachita *izi*.” O, izo ziribe kanthu kochita ndi izo; osati kanthu. Ine ndimadabwa nthawizina.

⁹¹ Kuno osati kale litali, ine ndinaona cho—cholengeza pamwamba, kumene msonkhano wina unali kubwera ku mzinda. Ndipo mawu a munthu, dzina la mwamunayo linalembedwa zilembo zazikulu kwabasi malo onsewo apo, monga *choncho*. Ndipo pansi, mu kangodya kakang’ono, anati, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse,” pansi patali mu ngodya. Mwaona?

⁹² Iwo anachotsapo kupatulika konse kwa Khristu, ndi kukuika iko pa munthu wina, kapena mpingo wina, kapena bungwe lina. M’bale, ine ndikukuuzani inu, inu mukhoza kulambalala ndi kukongola, zitsudzo za ku Hollywood, monga choncho, ndipo izo ndi za mwa mpingo. Koma, mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, Iye ndi Mmodzi woti azipatsidwa ulemerero. Ndiko kulondola. Tsopano ndicho choonadi, m’bale wanga wokonedwa ndi mlongo.

⁹³ Musati muyambe kukwiya pa ine. Inu mungokumbukira kuti ine ndikulalikira kwa inu. Ine ndikufuna kulalikira ngati kuti uwu unali ulaliki wotsiriza, ine ndikanati ndilalikirepo mu moyo wanga. Ine ndikufuna kulalikira, ulaliki uliwonse ine nditalalikire, ngati kuti ine ndinali munthu amene akufa akulalikira kwa anthu amene akufa. Ndipo, ine ndiri; nyali yanga ikuyaka mozima, tsiku lirilonse; yanunso ili, nayonso. Ndipo ife ndife zivundi zakufa. Ndipo ife tiyenera kukakomana

naye Mulungu wamoyo, ena mwa masiku amenewa, ndipo kulibwino ife tikhale mu kuwonamtima kwakuya pa izi.

⁹⁴ Ndipo basi mu kukongola, ndi kumangopitiriza, ndi kujowina mpingo, ndi kupita *kuno* ndi *uko*, kuchita mwa njira *iyi* ndi njira *iyi*.

⁹⁵ Ife kulibwino tizikhala nayo misonkhano ya kupemphera kwa kachitidwe-kachikale kunyumba zathu, ndi kumalirira kwa Mulungu, usana ndi usiku. Tsiku liri pafupi, “nthawi ya kupsyinjika, nthawi ya vuto.” Baibulo linati, “tsiku lamdima.” Ndipo ife tikukhala mu ilo.

⁹⁶ Momwe kuti munthu wamkulu uyu anapita kumeneko mwa kutengeka. Iye anadzilumikizitsa yekha ndi ofunda, ndi mzere wammalire, ndipo ankaganiza kuti iye anali kuchita chinachake chachikulu, ankaganiza kuti Mulungu anali kumodalitsa iye. Ndipo osazindikira kuti pomwepo iye anali kubweretsa mkati gulu lonse ili ndi iye. Chiyani? “Gulu lathu laling’ono, la Yuda—la Yuda kumtunda kuno, likanabwera uko ndi kudzilumikiza tokha ndi magulu aakulu a Israeli. Ife tidzakhala anthu amphamvu bwanji!”

⁹⁷ Ndi zimenezotu. Ndipo ndiwo mzere kumene wa chinyengo umene Mdierekezi akuwugwiritsa ntchito pakali pano, kuti abweretsemo wotsutsakhristu; basi motsimikiza monga ine ndaimira mu izi. “Ife tilumikizitsa kuyesetsa kwathu palimodzi.” Ife sitingakhoze kuchita zimenezo. Kodi awiri angakhoze bwanji kuyenda limodzi popanda iwo kukhala atagwirizana?

⁹⁸ United States uyu akupanga zofanana, chochitika chomwechomwecho ndi kulakwitsa komweko, pamene iye analumikizana ndi Russia mmbuyo muja. Pa nthawi imene iwo anali pafupi kukonzekera kukhala ndi nkondo, ndipo tinadzimangiriza tokha palimodzi ndi Russia. Ndipo tsopano inu mukuona zomwe ife tiri nazo, sichoncho inu? Iwo ali nazo ndege zathu ndi zonse za zinsinsi zathu, ndi mabomba athu a atomiki ndi chirichonse chiri kumeneko, kuti aziphulitsire izo kubwerera kwa ife. Chinthu chomwecho chikupita mwa uzimu!

⁹⁹ Ndiye ife tikupeza apo, atatha Yehosafati kupanga ubwanawe uwu, ndipo iwo anafunsira. Tsopano penyani, penyani dziko lakunja, iye anati, “Zedi, ife tiri nawo aneneri ambiri kumusi kuno. Ife tiri ndi seminare yodzaza iwo.”

¹⁰⁰ Iwo anapita uko ndi kukatenga anyamata amene anali ataphunzitsidwa, amene ankadziwa kuwerenga maganizo, amene ankadziwa zonse zokhudza izo. Anati, “Bwerani kuno tsopano, ndipo ife tikupempha ndi kufunsira Ambuye.”

¹⁰¹ Onse a iwo, zedi, mu kutukumuka kwawo mmaganizo kwachithupi anabwera pamenepo ndipo anati, “Tsopano, onani, ife... Inu pitani basi kumeneko. Ambuye ali ndi inu, ndipo Ambuye akakupatsani inu gawo ilo la dziko kumeneko. Ilo,

ndi loti likakhala lanu. Inu mukawakankhira Asiriya njira yonse kuwabweza. Inu mukachita zimenezo.” Mmodzi wa iwo anadzipangira yekha ngakhale mnyanga ziwiri zazikulu za chitsulo, ndi kuyamba kuthamanga pozungulira monga *chonchi*, kumati, “Tchi ndi chimene! Inu mukawakankhira Asiriya kutali.”

¹⁰² Koma, Yehosafati, basi wauzimuko mochuluka pang’ono, kuti apirire nazo zitsudzo za zovunda izo! Ndiko kulondola.

¹⁰³ Mulungu, tipatseni ife a Yehosafati ena ochuluka, odwala ndi otopa ndi zitsudzo izo za ku Hollywood kuno. Ndiko kulondola, kudzichititsa, kumanamizira kukhala chinachake chimene iwo sali; kumadzipangitsa, mwasewero, kumakokera mkati. Ndiyeno pamene iwo abwera mkati, ndi chiyani chimene inu muli nacho pamene iye anali mkatimo? Ngati kumufunsa munthu, “bwerani mudzasambire,” ndipo mu chipululu. Mopanda kanthu koma mchenga wa pa doko pa mutu wako, woti ukayambitse zowawa pambuyo pake!

¹⁰⁴ Tsopano zindikirani, kodi inu mungawabweretse iwo mu chiyani? Dona wina ananena kwa ine tsiku lina, “Mwamuna anati, ‘Ine ndikanamapita ku tchalitchi, koma chimene—ine ndikapeza chiyani pamene ine ndikanapita ku tchalitchi?’ Anati, ‘Zonse zomwe iwo amachita ndi kukonza mgonero wina, ndi zokhudza *izi, izo, ndi zina.*’” Ndipo donayo anati, “Ine ndinaima mwakakasi, pakuti ine sindinali kudziwa koti ndimutumize iye.” Ndi zimenezotu. Anati, “Ine ndikukhumba ine ndikanakhoza kupeza mpingo wachikale kumene iwo amayimba kwenikweni nyimbo zakachitidwe-kachikale ndi kumakhala mwaumulungu.”

¹⁰⁵ Ana ali ndi njala, iwo adya kuchokera motayira zonyansa. Izo ziri kwa Mpingo wa Mulungu wamoyo kuti uwadyetse iwo Mawu owona amoyo a . . . a Mulungu.

¹⁰⁶ Pamenepo, ndipo kukongola konse uko ndi zinthu; Yehosafati anati, “Kodi kulibeko mmodzi winanso?”

¹⁰⁷ “Mmodzi winanso?” anatero Ahabu. “Chabwino, inu mukumufunira chiyani mmodzi wina aliyense? Ife tiri nawo mazana anayi a opambana, osankhidwa, ophunzitsidwa, odyetsedwa-mwapamwamba, amuna -ovekedwa amene alipo mu dzikoli, ayima pano. Mmodzi aliyense wa iwo mu mgwirizano umodzi, ndi mtima umodzi, ndi liwu limodzi, akunena, ‘Pitani! Mulungu ali ndi inu.’”

¹⁰⁸ Ine ndikudabwa ngati United States sanakomane ndi chinthu chomwecho! Ine ndikudabwa ngati mpingo wa Mulungu sunakomane ndi chinthu chomwecho! Ine ndikudabwa. “Chabwino,” kunena, “penyani, iwo ali nako kupambana. Iwo akukhala ndi misonkhano yopambana, yayikulu. Iwo akunyamula zikwi pa nthawi.” Koma ine ndikudabwa ngati

palibe mmodzi wina basi! Ine ndikudabwa ngati palibe chinachake chosiyana!

¹⁰⁹ Ife tikupeza apo, ife tiri ndi otembenuka mtima zikwi makumi atatu mu masabata asanu ndi limodzi, ndipo masabata asanu ndi limodzi otsatirawo ife tiribeko mmodzi. Pali chinachake cholakwika penapake. Ndiko kulondola. Ndipo izo zonse ndi kukongola, kongodziveka. Dziko, kupyolera mu televizioni, kupyolera mu wailesi, kupyolera mu ziwonetsero za zithunzi, ndi zofalitsira izo kumeneko, zavunditsa fuko lino ndi zonyansa za Hollywood. Kulondola. Chirichonse chikufuna kukhala mu kukongola kwakukulu. Kodi icho si choonadi? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukudziwa ndizo zoonadi. Ife tiribe chinanso cha chipembedzo cha kachitidwekachikale kamene ife tinkakhala nako zaka zapitazo. Ndi chifukwa kuti izo zakhala zitalekereredwa. Ife tifika kwa izo, mu mphindi chabe, inu muwona.

¹¹⁰ Motani, ndi chithunzi chokongola bwanji, kapena chithunzi chokondoweza, ine ndiyenera kunena. Ndipo pano pakubwera Yehosafati uyu, anati, “Inde, ine ndikuwaona iwo onse. Iwo ali, mmodzi aliyense, ali nawo madigirii,” ndipo chirichonse chimene icho chinali. “Iwonso akhala ali aneneri. Iwo ndi alaliki opambana. Iwo ali ochokera ku makoleji aakulu. Ndipo iwo ali zonse izi. Iwo ali ochokera ku sukulu yayikulu ya aneneri, ndi chirichonse. Iwo onse ali ndi mgwirizano umodzi. Ndizo zoonadi. Koma kodi kulibe uko mmodzi wina chabe?”

¹¹¹ “Chabwino, inu mufunira chiyani mmodzi winanso, pamene mazana anai akupereka kuvomereza pa nthawi imodzi?”

¹¹² Koma mwamuna ameneyo, patali panso mu mtima mwake, anali ndi Mulungu. Ndipo iye ankadziwa kuti apo panali chinachake cholakwika cha izo. Inde, bwana. Iye anadziwa kuti apo panali chinachake chovunda. Motani? Ndiroleni ine ndikupatseni inu... Lemba silimanena izo, koma pano pali zimene ine ndikupeza. Ine ndikudziwa kuti—kuti Yehosafati ankadziwa kuti wachinyengo uyo kumusi uko, Ahabu, kuti iye sanali mwabwino ndi Mulungu. Ndipo Eliya anali atalosera Mawu a Mulungu kwa iye. Ndipo Mulungu akanakhoza bwanji kudalitsa chimene Iye anachitemberera? Ameni.

¹¹³ Ine ndikunena chinthu chomwecho lero, mzanga. Ndipo Mpingo wa Mulungu wamoyo, yemwe akuima moona kwa Mulungu, adzanena chinthu chomwecho. Inu simungakhoze kusakaniza Mafuta ndi madzi pamodzi ndi kuchitcha icho chipulumutso. Inu simungakhoze. Inu muyenera kudzilekanitsa nokha, m'bale. Chinachake chiyenera kuchitika. Ngati pali chiyembekezo chirichonse chatsalira, ife tiyenera kuchita chinachake, ndi kuchichita icho mwamsanga; pakuti, ora, Mkwatulo uli pafupi.

114 Zinthu ziri kuwunjikana, chirichonse, ndipo mpingo wapita patali chotere. Iwo akuwerenga magazini a mitundu yonse, mabuku, nthano, ndi chirichonse. Ine ndikhoza kupita lero ku. . . Ine ndikhoza kupita ku mpingo, ndipo ine ndikhoza kunena, “O, ndi angati akudziwa. . .” Iwo amadziwa nyimbo iliyonse, chitachitika chimodzi cha zitsitsimutso zazikulu izo. “Tsopano, nyimbo yakuti-yakuti ili pa tsamba lanji—lanji?” Iwo amadziwa zimenezo. Iwo amadziwa yemwe iye ali. Iwo amadziwa yemwe akupikisana nawo Uprezidenti, ndi amene akupikisana nawo *izi*, ndi akatswiri a pa kanema angati akwatira, *izi* ndi *izo*, *zimzake*. Koma, Mawu a Mulungu, iwo sakudziwa kanthu kake. Ndi zimenezotu. Kotero ife tikuwapatsa zawo. . . Ndipo, komabe, iwo amadzinenera kuti ali Akhristu.

115 Ndipo anthu si oti ungawatsutse. Ndi zochokera kuseri kwa nsanja, ndi kumene izo zikuchokera. Chimodzimodzi. Izo zikuchokera kuseri kwa nsanja. Iwo amawaphunzitsa iwo mitundu yonse ya kayimbidwe, ndi mitundu yonse ya *izi* ndi *izo*, ndi mabungwe, momwe angakupangire iwe kulalikira, ndi chirichonse monga chomwecho. Ine ndikudabwa ngati izo zimalipiridwa? Palibe zotsutsa izo, koma ine ndikudabwa ngati ndicho chofuna cha Mulungu.

116 Pamene, Yesu anati, “Kupatula munthu akhala wobadwa mwa madzi ndi Mzimu, iye mwa njira iliyonse sadzalowa mu Ufumu. Iye amene kwa-. . . ati adzatsatire pambuyo pa Ine, msiyeni iye adzikane yekha, ndi zosangalatsa zake za chidziko, kutenga mtanda wake ndi kutsatira pambuyo pa Ine.” *Mtanda* ndi choyimira cha “imfa, kupweteka.” “Iye amene ati adzakhale Mkhristu, msiyeni iye adzivule yekha za malingaliro ake omwe. Msiyeni iye adzivule yekha za zintchito zake. Msiyeni iye adzivule yekha za chirichonse, kudzikana yekha; ndi kutenga mtanda wopatulika uwo, ndi kunditsata Ine tsiku ndi tsiku. Iye amene ati adzatsatire pambuyo pa ine, msiyeni iye achite zimenezo.” Ndizo zimene Yesu ananena.

117 Koma, lero, ife timati, “Aliyense akhale ndi nthawi yayikulu. Aliyense awombe manja ake. Aliyense afuule, ‘Aleluya!’ Aliyense achite *izi*.” O, momwe ife tiriri ndi gulu la mkangano! Amen. Mulungu. . . Ife tiri ndi nyimbo zatsopano izi ndipo timayimba izo mofulumira kwambiri, mwakuti izo zimawoneka ngati ife tipite kupyola mu khoma ndi izo, kapena chinachake chonga icho.

118 Pamene, ine ndikuganiza, ngati ife tikanakhala tikuyimba *Pafupi*, *Mulungu Wanga*, *Kwa Inu*, zikanakhala ziri gawo lonse zabwinoko kwa Mpingo; nyimbo zakachitidwe-kachikale.

119 Kutengera anthu ambiri a dansi ya orchestra, mnyamata wina mu dansi ya orchestra kuno akusewera, usiku watha, ndipo usikuuno cha kuno akusewera mu mpingo wa Mulungu wamoyo? Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu. Msiyeni munthu

ameneyo atsimikiziridwe, poyamba, ndipo msiyeni iye abweretse chipatso, chokwanira cha kulapa, kuti asonyeze kuti iye ali mwabwino ndi Mulungu.

¹²⁰ Iwo akubweretsa dziko la jazi mpaka pa nsanja kumene. Iwo akubweretsa Hollywood, kulalikirira kokongoletsa, mpaka pa nsanja pomwe.

¹²¹ Bwanji, kodi ine sindinakhale mu mzinda wanu wokongola, masabata angapo apitawo, mu Louisville, Kentucky? Mtima wanga kusweka! Pamene iwo onse anali atakhala pamene, ololera kuwona zozizwitsa za Mulungu; ndipo mwamsanga pamene iwe ulalikira Uthenga, iwo amakhoza kukhuta, mu mphindi, ndi kutembuzira misana yawo ndi kuyenda kutuluka mnyumbamo. Ndithudi. Iwo sakuwufuna Iwo. Mitima yawo yawumitsidwa. Kutuluka panja; ndipo ambiri a iwo, Achiprotestanti, nawonso, amene amapita ku mipingo ya Chiprotestanti. Koma iwo anakhala akukhuta... kudzazidwa mokhuta ndi kukongola ndi chirichonse monga choncho, zamkhutu ndi zampingo, mpaka iwo sakudziwa kanthu za Mzimu wa Mulungu wamoyo. “Okhala nawo mawonekedwe a umulungu, ndi kumakana Mphamvu yake.”

Ndi tsiku lotani limene ife tikukhalamo! Penyani kumene izo zikuwunjizikana.

¹²² Yehosafati anati, “Ine ndikudziwa, Ahabu. Uko kuli alaliki anu mazana anai. Iwo onse ndi anthu amawonekedwe abwino, mmodzi aliyense wovekedwa ndipo tsitsi lawo lopesedwa mwaukhondo, ndi chirichonse, chinachirichonse iwo angakhale. Iwo akhoza kukhala ndi ma D.D. awo. Iwo akhoza kukhala ndi mitundu yonse ya madigirii. Iwo akhoza kudziwa Malemba, kuchokera A mpaka Z. Koma kodi inu mulibe mmodzi winanso, penapake? Ndipo kodi kulibe uko mmodzi wina chabe, penapake?”

¹²³ Iye anati, “Inde, pali mmodzi winanso, koma ine ndimamuda iye.” Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu. “Ine ndimamuda iye.” Kumbukirani, Ahabu anali munthu wachipembedzo, ndipo awa anali aphunzitsi achipembedzo, koma iwo ankamuda munthu uyu amene anali nacho Choonadi. Anati, “Ine ndimamuda iye.” Anati, “Iye nthawizonse amageya chinachake motsutsa ine.” Iye akanakhoza bwanji kudziletsa kuchita zimenezo, pamene Mawu a Mulungu anali atamutsutsa iye?

¹²⁴ Iwe ungakhoze kukhala chete chotani ngati iwe uli mwamuna wa Mulungu, kapena mkazi wa Mulungu, ndi kudziwa ndi kuliwona tchimo ndi zinthu, zitawunjikana ndi kulemetsedwa, ndi chirichonse monga choncho; ndi kuwona miyoyo ya anthu ikupita ku gehena, mamilioni pa tsiku, ndi kuyima duu? Iwe sungakhoze kuchita zimenezo.

Winawake ananena kwa ine kuno, “Inu mukuganiza inu mungakhoze kuziletsa izo?”

125 Ine ndinati, “Ayi. Ine sindingathe kuziletsa izo, chifukwa Mulungu anatero. Koma tsiku lina, pa Malo Achiweruzo, iwo akasolola chowonetserapo chachikulu, kuwalitsira pa kamera kutali, ndipo kujambula kwa tepi uko kukaseweredwa. Ndipo ine ndikaima ndi kukamvetsera pa iyo, ndipo ine ndikufuna kudzamva liwu langa likuchenjeza motsutsa izo. Mulungu adzandiweruza ine pamene liwu langa likubwera motsutsa izo.” Inde, bwana. Pamene ife tikuwona moyo uno, m’badwo uno, ukubwerezedwa kachiwiri uko pa Chiweruzo. Ndithudi. Ife tikukhala mu nthawi yowopsya. Ndipo ndi izo apo.

Ndipo ife tikumuwona iye; iye anati, “Kodi kulibe uko mmodzi winanso?”

126 Iye anati, “Inde, koma ine ndimamuda iye, pakuti iye nthawizonse akulosera zoyipa motsutsa ine.”

127 Iye angakhoze bwanji kudziletsa kukulalikira zinthu zolimba zimenezo, pamene iye akuwona izo zikupitirirabe? Kumuwona Ahabu akukhala moyo monga iye anali ndi kumachita monga iye anali, ndi kumawabweretsa anthu momwe iwo aliri!

128 Angathe bwanji mwamuna wa Mulungu, kapena mkazi wa Mulungu, kudziletsa kuti afuule ndi kudzudzula tchimo kuchokera ku mbali iliyonse? Pamene, iwo akuwona alaliki ofunda awa, ndi okongoletsa, ndi ophunzitsa, ndi zina zotero monga izo, kumangowalola anthu kumapita ku gehena, mwa mamilioni, pansi pa chinyengo; zochuluka za . . . ngakhale mwa anthu a chiyero. Ine sindikuyankhula mochuluka kwambiri zokhudza Amethodisti ndi Abaptisti, ndi zinthu monga izo; iwo ali nazo izo, nawonso. Koma izo ziri kumene mu malo anu omwe. Mai!

129 Iwo adzabwera ku nsanja, ngati china chirichonse kupatula Akhristu, kumakhala moyo ngati china chirichonse, ku mayiko onse ndi zinthu, ndiye iwo amachitcha icho “chipembedzo.” Ndi chipembedzo, koma chiri kutali kwambiri ndi ku chipulumutso cha Ambuye. Ndiko kulondola. Iwo angokhala nawo anthu mpaka langokhala gulu lalikulu la odzichititsa. Ndiye mwamsanga pamene kudzichititsako kupitirira, ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwe sungakhoze kupeza mmodzi wa iwo; mpingo umakhala wopanda anthu. Koma ngati munthu amakonda Mulungu, iye adzadzaza pokhalapo pake mu tchalitchi, nthawi iliyonse. Iye sangakhoze kujomba kwa iwo. Ndiko kulondola.

130 Tsopano zindikirani mphindi pang’ono chabe. Ine ndiyesa kufulumira, kufika molunjika ku nsonga tsopano, chifukwa nthawi yanga ikupita kutali.

Zindikirani, ndiye iye anati, “Kodi uko kulibe mmodzi winanso?”

¹³¹ Iye anati, “Inde, koma ine ndimamuda iye. Iye nthawizonse amalosera motsutsa ine. Iye akumanena zinthu zoyipa motsutsa ine.”

“Chabwino,” anati, “pitani mukamutenge iye.”

Iye anati, “Dzina lake ndi Mikaya.”

¹³² Koma munthu uyu anali ndi chipembedzo chokwanira kuti adziwe kuti anyamata awa sanali kulondola.

¹³³ Ndipo munthu aliyense amene anakhudzidwapo, kugunda kochepa, mwa Mzimu wa Mulungu, amadziwa kuti zinthu izi, zimene zimatchedwa Chikhristu lero, siziri zolondola. “Iwe sungakhoze kulikonda dziko, kapena zinthu za mdziko; ngati iwe utero, chikondi cha Mulungu sichiri mwa iwe.” Baibulo linanena choncho.

Tsopano yang’anani. Iye anati, “Pitani mukamutenge iye.” Ndipo iwo anapita kumeneko.

¹³⁴ Ndiyeno iye anatumiza mthenga wachikale wamng’ono motsatira, dikoni wa mpingo, mwinamwake, kapena winawake, anapita cha kumeneko ndipo anati, “Tsopano yang’ana, Mikaya, ife tikubweretsa iwe kuno pamaso pa Ahabu ndi Yehosafati. Tsopano iwo onse akhala kumeneko. Ndipo iwo ndi amuna opambana tsopano. Iwo ndi aphunzitsi ndipo iwo ndi masakolala. Ndipo iwo ali ndi digirii zawo, ndi zina zotero. Ndipo iliyonse ya seminare yathu, uliwonse wa mipingo yathu kuno, ili yangwiro pa mgwirizano kuti ichi ndi chifuniro cha Ambuye. Tsopano iwe unene chinthu chomwecho chimene iwo akunena, ndipo, ine ndikukuuza iwe, iwe udzavala bwino ndi kukwera mu galimoto ya Cadillac. Ine ndikukuuza iwe, iwe udzakhala basi munthu wamkulu ngati iwe uti uchite zimenezo. Inde, bwana. Iwe udzalemera.”

¹³⁵ Mikaya anati, “Momwe Ambuye Mulungu ali moyo, ine ndidzanena kokha chimene Mulungu anena.” Amen. Eya. O, apo pali munthu wa pa mtima panga. “Ine ndikhoza kumadya mkate ndi madzi,” chimene iye anachita, “chifukwa chakuchita izo.” Iwe ukhoza kuti anakanthidwa pa tsaya limodzi ndi limzake, china chirichonse, koma iye anawawuza choonadi ndipo anayima ndi icho. Mulungu anatsimikizira icho kukhala choonadi. Iye sanali wotchuka kwambiri, koma iye ankamudziwa Mulungu.

¹³⁶ Anamubweretsa Mikaya wamng’ono wakale cha kumeneko. Iye anati, “Chabwino, Mikaya, iwe ukunena chiyani za izi?”

¹³⁷ Iye anati, “Pitani kumeneko. Pitani kumeneko.” Anati, “Pitani uko, mu mtendere. Pitirirani uko, kapambaneni, ndicho chimene ine ndikufuna kuti inu muchite. Koma ine ndinaona Israeli ngati nkhoa, wopanda m’busa, pa phiri, womwazika. Ndi zimenezo,” iye anatero.

138 Ndipo pamene iye anachita zonga zimenezo; ndipo Ahabu anatembenuka chozungulira, ndi Yehosafati. Anati, “Ine ndinakuuza chiyani iwe? Woyera-wodzigudubuza uyo, kapena chiyani,” mundikhululukire ine, “kapena chirichonse chimene iye anali, munthu uyo ananena zimenezo! Ine ndinakuuza chiyani iwe? Mnyamata ameneyo akanaloseera kokha choyipa monditsutsa ine. Ine ndinakuuza chiyani iwe? Iye akanangotsutsa kokha mpingo wathu, ndi kutsutsa atumiki athu, ndi kutsutsa njira yathu ya chipembedzo. Kodi ine ndinakuuza chiyani iwe? Iye akananena zimenezo. Ine ndikumudziwa iye. Ine ndinkawadziwa bambo ake asanabadwe iye.” Ameni. [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kamodzi—Mkonzi.] “Ine ndinkawadziwa bambo ake asanabadwe iye.” U-nhu, inde, bwana, mwamuna weniweni wa Mulungu. Anati, “Ine ndimadziwa kuti iye akananena zimenezo.”

139 Ndipo kotero ndiye iye anati, “Inde,” anati, “Ine ndinawona Israeli ngati nkhoa, atabalalika, wopanda m’busa, pa phiri.” Ndipo kotero ndiye iye anati, “Ine . . .”

140 Ndiyeno mmodzi wa anyamata awo yemwe anali ndi nyanga zazikulu, amapita kukamukankha. Mlaliki anayenderako ndi kumukokera Mikaya kuseri, ndi kumukang’antha iye pakamwa molimba monga iye akanakhozera, anati, “Ndi njira iti imene Mzimu wa Mulungu unapita pamene Iwo unatuluka mwa ine? Ngati iwe ukudziwa.”

141 Anati, iye anati, “Dikira mpaka iwe utakakhala mu ndende ya kuno, ndipo iwe udzadziwa njira imene iwo unapita.” Ndiko kulondola.

142 Dikirani mpaka Russia atakhala kunjira kuno, atalanda mafuko ndi zinthu ngati zimenezo, ndi dziko ili, chifukwa cha kubwerera mmbuyo kwake, ndipo inu mudzawona chimene chinali cholondola ndi cholakwika. Ndiko kulondola. Inu mudzawona ngati chipembedzo chanu chofunda chiti chidzapindulitse, kapena ayi.

143 Siyani fuko ili lifike ku misonzi, osati kubwera ku kuseka ndi seweru. Mulole fuko ili lidze ku maondo ake, mu kulapa. Ndicho chimene ife tikusowa. Osati chitsitsimutso kuti titengere anthu ochuluka kwambiri mu mpingo. Ife tikusowa kutseka malo ogulitsira mowa aliwonse, kuletsa kusuta kwa ndudu konse, kugwetsera pansu mafakitare. Kuyambitsa msonkhano weniweni, wakachitidwe kachikale, wa Mzimu Woyera; kumene amuna ndi akazi, usana ndi usiku, agona pa nkhope zawo, akulira. Ine ndikukuuzani inu, iwo udzakhala mthunzi wawukulu umene fuko ili linayamba lakhala nawo. Ndizo zoon.

144 Mulole Branham Tabernacle isiye zopusa zake. Mulole iyo ifike kumbuyo kuno pa guwa ndi kuyanjana naye Mulungu.

Kuyanjana ndi oyandikana nawo, ndi zina zotero monga choncho, ndi kufika pabwino ndi Mulungu. Inu simukanakhala ndi mikangano iliyonse ndi kupitiriza; iwo adzakhala malo okoka kwa dziko. Ndiko kulondola. Tsopano, ndicho choonadi.

¹⁴⁵ Ndiye iye anati, “Ndi njira iti imene Mzimu wa Mulungu unapita pochokera kwa ine?”

¹⁴⁶ Ndipo Mikaya anati, “Ine ndinawona Mulungu ndi khamu Lake, upo Wake, utakhala mu Ulemerero.”

¹⁴⁷ Inu mukudziwa, Mulungu amakhala ndi upo kumwamba Uko, kamodzi mu nthawi. Iye, Iye amabweretsa Ake—Zinthu Zake Zaungelo ndi kuchititsa—upo, kamodzi mu nthawi, Kumwambako.

¹⁴⁸ Ndipo iye anati, “Ine ndinamuwona Iye atakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anthu onse anali atayima pa dzanja lamanja ndi lamanzere la Iye.” Ndipo anati, “Iwo anali akukambirana, ‘Kodi ndi ndani yemwe ife tingakhoze kumutenga kuti apite pansu ndi kukamunyenga Ahabu, kuti amutengere iye kuno ndi kuti akwaniritse uneneri wa Eliya? Mulungu wanena kale chotero, zimene zimati zidzachitike, kotero ife tingowona yemwe angakhoze kupita pansipo.’”

¹⁴⁹ “Ndipo mzimu wabodza unatulukira kuchokera pansu,” zoonza, kuchokera ku gehena, “unabwera pamaso pa Mulungu ndipo unati, ‘Ine ndipita pansipo, ndipo ine ndikalowa mwa alaliki amenewo ndi kuwapangitsa iwo onse kulosera bodza.’” O, kodi izo zinawafufumitsa iwo! Kodi izo zinawapangitsa iwo kumverera mwachirendo, pamene, “Iwo anati, ‘ine ndipita pansipo ndi kukawapangitsa alaliki amenewo, mmodzi aliyense wa iwo, kuti anenere bodza.’” Ndipo iye anafika pansu ndipo analowa mwa alaliki amenewo, ndipo iwo anayamba kunenera bodza.

¹⁵⁰ Ndipo, m’bale, Mulungu yemweyo akulamulira pa Mpandowachifumu womwewo lero. Ndipo mzimu wabodza womwewo wachita chinthu chomwecho lero, kunenera mabodza.

¹⁵¹ Iwo anapitirira kunena, “Mtendere, mtendere, mtendere,” itatha Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse.

¹⁵² Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu kumene izo zinachokera. Mu Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse, pamene France kumeneko anachoka kwa Mulungu, mu kudyerera kwawo mma ’90 achisangalalo, ndi kuyamba . . .

¹⁵³ Tsopano ine nditenga pang’ono pa makhalidwe, kotero inu mungokhala chete kwenikweni kwa maminiti pang’ono.

¹⁵⁴ Onani, kumbuyo uko, mu kuyambirira, uko mu France, kumeneko ndi kumene uthakati ndi uve zinayamba poyambirira. Ngati panakhalapo una wa khoswe mu dziko, ndiwo Paris, France. Ndipo ine ndayenda pafupifupi ambiri a iwo, ndipo

ndiwo malo oyipisitsa amene ine ndinawawonapo. Ndipo London, England sali womupatula mochuluka. Ndipo United States akubwera kumene mu mzere ndi iwo. Ndiko kulondola. Uko iwo ali.

¹⁵⁵ Nthawi iliyonse imene inu mumaphwanya makhaliidwe a umayi, inu mumaphwanya fupa la nsana wa fuko.

¹⁵⁶ Kuno inu mupiteko, mu maiko awo omwe, ndi kunena kuti ndinu mishonare, iwo samakonda . . . Kunena, “Inu mutiuza ife chiyani, momwe tingambire nyimbo zoyipa zokhudza akazi athu, kapena zokhudza asungwana athu? Inu mutiuza ife momwe tingawasudzulire akazi athu? Kutiphunzitsa ife momwe tingamwere kachasu ndi kupita njira imene ife timachitira?” Ndicho chimene ife tiri.

¹⁵⁷ Ife timadzitcha tokha fuko la chipembedzo, fuko la Chikhristu. Chabwino, “achikunja” awo mu Africa akhoza kutiphunzitsa ife makhaliidwe, momwe tingakhoze kukhalira. Malo ovunditsitsa, mu United States, kapena dziko, pafupifupi, ndi fuko lino, momwe ilo liliri. Ine ndine Wachimerika, kwenikweni. Koma, m’bale, ine sindingachitire mwina . . . ? . . . asanati Ahabu kapena Yehosafati, ndipo ine ndiyenera kunena chimene Mulungu amanena kuti ndi Choonadi. Ndicho chimene mpingo ukusowa kuyima nacho, lero. Ngati izo zibwera pakati pa fuko ndi Mulungu, ndi Mulungu, nthawizonse. Inde, bwana.

¹⁵⁸ Zindikirani, mu France, iwo anayambitsa kuvunda kwawo konse, ndi kumapitirira mwa njira imene iwo anakhalira kumeneko. Ndiyeno Mulungu anatomiza Germany kwa iwo, kukawamenya iwo pang’ono pokha. Ndiye ife tinapita kumeneko kukapulumutsa chikopa chawo. Ndipo mwamsanga pamene ife tinachita zimenezo, ndipo tinapambana nkhondoyo, tinatumiza Ajeremani kumbuyo, tinali ndi mtendere ndi France, kodi iwo anatembenukira kwa Mulungu? Ayi, bwana. Akazi, mowa, chinyengo, tchimo ndi uve mpaka mu makha!

¹⁵⁹ Ndiye kodi iwo anachita chiyani? Nchiyani chinachitika? Apa ndi pamene ife tinayambira. Mdierekezi anakhazikitsa malikulu ake kumeneko. Uko ndi kumene iye anayambira, komwe uko, kulichotsera khalidwe dziko, kuyambira ku Paris, France.

¹⁶⁰ Ndiye, ngati inu mutazindikira, iye sakanakhoza kulowa muno kupyolera mu utumiki, kotero chinthu chimene iye anachita chinali kubwera mkati ku Hollywood konkuno. Iye anakhazikitsa wake Holl- . . . Iye anakhazikitsa malikulu ake cha kuno mu Hollywood. Mdierekezi anatelanso kuno, zaka zingapo zapitazo, zaka khumi ndi zisanu kapena makumi awiri zapitazo, ndi ankhondo ake aakulu, ndipo anapita, anagunda mu Hollywood, California. Ndipo iye wawukira United States ndi mphamvu zake za ziwanda. Kulondola! Mafashoni athu onse amachokera ku Paris. Iwo analowa mu Hollywood, mpaka pa

zowonetsera. Asungwana aang'ono awa ndi anyamata aang'ono, ndi zinthu, anafika kuno, iwo amawonera masewero a pa chowonetsera awo.

¹⁶¹ Ana aang'ono abwino, anthu abwino aang'ono, palibe chowatsutsa iwo. Mulungu adalitse mitima yawo yaying'ono! Mtima wanga umawawukhira iwo.

¹⁶² Ndipo komwe kuno mu mzinda, ine ndinali kuyankhula kwa wanga . . . mmodzi wa . . . Mnyamata wanga, tsiku lina, iye anati, “Adadi, ngati alipo basi anyamata ena kuzungulira kumeneko, mu tawoni, amene anali ndi Mzimu Woyera,” ndi zina zotero. Inu mumadabwa chifukwa chimene ine ndinali kuchokako ku Denver, Colorado, kapena kwinakwake monga choncho? Kutengera ana anga kwinakwake kumene kuli gulu la anthu amene amalirira kwa Mulungu! Nchimene ife tikusowa, m'bale!

¹⁶³ Dziko lino, fuko lino, mzinda uno, malo ano, afika popanda makhalidwe kwambiri mpaka iwo ndi omvetsa chisoni. Ngati ine ndingakhoze chabe kufotokoza pakali pano chimene ine mwamtheradi ndimadziwa kuti ndi choonadi pomwe pano, icho sichikanakhoza ngakhale kukhala choyenera kuperekedwa pamaso pa omvera osanganikirana. Kapena, momwemuno mu mzinda womwe uno pakali pano; osati kuno kokha, koma malo ena, kulikonse, izo zayamba kubwera mwa wamba . . .

¹⁶⁴ Chifukwa chiyani? Anthu . . . Penyani, amzanga, izo zafika mwachinyengo chotero. Izo zafikamo mophweka kwambiri, mpaka izo zimangokubanikitsira iwe pansi. Mdierekezi anakonda kukhala mu mafashoni. Iye mwina sanatuluke mu mafashoni, koma iye sanamuthere malonda, ine ndikukuuzani inu zimenezo. Iye akadali ndi malonda.

¹⁶⁵ Penyani, lero. Ife timatenga, monga ine ndinanena kanthawi kapitako, zokhudza dona wamng'ono, msungwana wamng'ono wakale ali ndi duwa. Mwa chitsanzo, duwalo, ndi lokongola; ilo liri pamenepo kuti lizipenyedwa, ndizo zoono. Ndipo izo ziri basi ngati mpingo, iwo uli pamenepo kuti uzipenyedwa. Monga mkazi wamng'ono wokongola, iye ali pamenepo kuti azipenyedwa. Ndiko kulondola. Koma ngati iye . . . Iye ali wabwino, icho iye ali kwa mwamuna wake, iye—iye ali bwino. Koma ngati iye alibe lupanga la makhalidwe litatulukira pamenepo kuti lizimuteteza iye, iye amakhala chobwerekera kwa mudzi ndi anthu okhalapo; amatsika chotero ndi mochititsa manyazi ndi movunda mpaka agalu sangayang'ane pa iye. Ndiko kulondola.

¹⁶⁶ Ndipo chinthu chomwecho kwa mpingo wa Mulungu wamoyo! Iwo amabwera kunja kuno ndi kuyesa kukongoletsa ndi kuzikonza okha, ndi kumachita ngati . . . Iwo amawavula akazi awo kuno, kumene . . . ndipo anthu samazindikira kuti adierekezi awa akuwukira makomo anu.

¹⁶⁷ Mwa oyandikana nawo anga omwe tsiku lina, dona wamng'ono yemwe ine ndikuganiza ndi mkazi wabwino . . .

Ndipo iye ndi mkazi wokwatiwa, ali ndi mwana. Ndipo mkazi wamng'onoyo anabwera kumeneko. Mwamuna amabwera pansu mu msewu kudzachita ntchito ina, ndipo dona wamng'ono uyu anatuluka kunja uko atavala zovala zazing'ono zambekesha zakale izo, zinali zonyansa.

¹⁶⁸ Uku ndi kuyankhula kosayenera Tsiku la Anakubala. Koma, m'bale wanga, ndirole ine ndikuwuze iwe chinachake. Amayi, bwererani mmbuyo kuti mukhale amayi kachiwiri!

¹⁶⁹ Ngakhale kwa mnyamata wamng'ono kwambiri anali kuchezero oyandikana nawo athu, anabwera mkati ndipo anatiwuza ife za izo, "Tayang'anani kunja uko!"

Ine ndinati, "Chabwino, sindizo kanthu."

¹⁷⁰ Mkaziyo ndi mkazi wabwino. Ine sindikunena kuti iye ndi wopanda makhalidwe. Koma, chinthu cha icho chiri, pali mzimu wa uthakati, wauve pa iye, ukumupangitsa iye kuchita zimenezo, ndipo iye sakudziwa zimenezo.

¹⁷¹ Kodi ndi chiyani mu dziko chimene mayi angafune, ngakhale aliyense, kuvala zovala zazing'ono zakale zonyansa izo, ndi kudziwongolera okha kunja pamaso pa mwamuna? Ndinu wokongola, mlongo. Ndinu wokongola, mayi. Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha inu. Koma, ndinu wokongola, koma inu mulibe Mzimu Woyera pamenepo woti utetezere makhalidwe amenewo. Inu mukanakhala bwino ngati inu mukadakhala wosakongola palibe yemwe akanayang'ana pa inu, ndi kupita mukwamba. Ndiko kulondola. Ndizo zooni. Penyani zimene inu mukuchita; makhalidwe amenewo.

¹⁷² Tsopano, chimene izo ziri, Mdierekezi wabwera mkati ndipo iwe wawauza anthu zinthu zimenezi. Iye wafika mwa alaliki; iye akutengera za ku Hollywood. Asungwana ndi aang'ono—madona aang'ono, iwo akutengera zaku Hollywood. Zinthu zopambana zimene iwo ali nazo mu dziko lero, zamakhalidwe kwambiri zimene iwe ungakhoze kuzimva, ndi kuyankhula za zoyankhulidwa pa wailesi.

¹⁷³ Mkazi wina wachikulire ngati Abiti Kay Starr, palibe chotsutsa iye; koma kuwona mkazi wachikulire, usinkhu wa zaka makumi asanu, ndi yense, ndi zovala zake zonse zitakankhidwira pa iye, ngati kuti iye anatsanuliridwa mu thumba la ufa. Ine sindikunena izo mwa nthabwala, chifukwa ine ndikuyankhula motsutsa zinthu zimenezo. Koma mkazi kuchita monga choncho, ndi kuimirira ndi kukhala chitsanzo kwa akazi aang'ono a Chimerika, ndi chobwerekera kwa fuko lathu. [M'bale Branham agogoda pa guwa kasanu—Mkonzi.] Ndi Mdierekezi.

¹⁷⁴ Anyamata ngati Arthur Godfrey ndi iwo akuthamanga kuzungulira kuno, akuchita zinthu zimene iwo amachita, ndipo munthu wodziwika kwambiri mu dziko monga choncho, ndipo, bwanji, ndi chamanyazi.

¹⁷⁵ Aleluya! Ine ndikunena izo chifukwa ine ndikumverera kuti Mzimu Woyera uli pano. Kuwukiridwa kukuchitika, basi kukusesa ku nyumba ndi nyumba, ku malo ndi malo, ku mpingo ndi mpingo, kwa munthu ndi munthu.

¹⁷⁶ Ana, mu Dzina la Yesu Khristu, amawuka ndi mayimidwe a khalidwe la chitsitsimutso ndi Ambuye Yesu Khristu, ndi kunena, “Ine nditenga njira ndi onyozedwa apang’ono a Ambuye.” Inde, bwana. “Ine ndikhala mayi weniweni.” “Ine ndikhala bambo weniweni.”

Pamene dziko lonse, ndi konse kozungulira,
pozungulira moyo wanga wonse ukupereka
njira,
Ndiye Iye ali chiyembekezo changa chonse ndi
chikhazikitso.

Pakuti pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine
ndikuimapo;
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira,
Maziko ena onse!

¹⁷⁷ Nchiyani chapangitsa zinthu zonse izi? Nchiyani chapangitsa atumiki kumachita monga chomwechi? Nchiyani chapangitsa alaliki kumanenera bodza ili kwa anthu?

¹⁷⁸ Nchiyani chinachita izo, zaka zapitazo, kuti inu anthu Amethodisti... Pamene John Smith wachikulire ananyamulidwira ku guwa lake, kuti akalalikire Uthenga, ndipo iye analalikirira ulaliki wawufupi wa maora anai. Ndipo iye anati, “Vuto la izo ndi, kuti mtima wanga ukusweka.” Iye anati, “Ana aakazi Amethodisti akuvala ngakhale mphete pa zala zawo.”

¹⁷⁹ Ndipo, lero, iwo avala akabudula ndi zovala zakale zauve. Ndipo iwo adzakhala mbulanda mwangwiro, mu zaka zina zisanu, ngati chinachake sichichitidwa. [M’bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ndi chiyani chinachitika kwa inu alaliki Amethodisti, inu a Chikampubelo, inu Abaptisti? Inde, bwana. Ndi Mdierekezi, waponyera pansu mphamvu zake, ndipo iye ali ndi ziwanda zake kunjira kuno.

¹⁸⁰ Ndipo inu simukuzindikira izo, inu mukusuta ndudu, inu akazi, ndi kumachita njira imene inu mukuchitira kunjira uko, ndi kumamwa ndi kumapitiriza mwa njira imene inu mukuchitira. Inu simukuzindikira kuti inu mukuika chiphe mukachitidwe kanu, ndi kuwononga m’badwo wonse umene uti udzakutsatireni inu, ngati pali chinthu choterocho. Magawo makumi asanu ndi atatu mphambu asanu pa zana mwayi wochulukira kuti atenga khansara, pa kusuta ndudu, ndipo inu mwadala mumasunthira kumene kupita mu izo. Ndipo mipingo imavomereza izo.

¹⁸¹ Mu mipingo yayikulu ya Baptisti kuno, posachedwapa. Ine ndikumenya Abaptisti. Ine ndiri nawo ufulu wochitira izo; iwo amakhala ngati amatsamira ku mbali imene ine

ndinachokerako. Koma pamene iwo anachita kumapereka kupuma pakati pa msonkhano wa Sande sukulu ndi msonkhano wolalikira, kotero kuti abusa ndi onse akhoza kutuluka panja ndi kukasuta, ndipo msewu umandandidwa ndi amuna ndi akazi akusuta ndudu. Mdierekezi wachita zimenezo. Ndiko kulondola.

¹⁸² Ndiye, kuno mu mzinda wathu womwe, mmodzi wa atumiki athu odziwika, kumusi komwe kuno mu New Albany, pa bwalo lamasewero ili, kuti mmodzi wa atumiki athu odziwika a mzinda akutsogolera dongosolo la kwasakwasa, kuti awabweretse amuna ndi akazi pa nsanja.

¹⁸³ Sindikusamala chimene dziko liti linene, ine sindikusamala momwe inu mumayesera kuyanana pozungulira ilo; m'bale, palibe mwamuna wa magazi-ofiira angadzikokere kwa mkazi wa mwamuna wina, ndi kumverera chimodzimidzi. Inu mukudziwa ndicho choonadi.

¹⁸⁴ Iwo atenga akazi athu, ndi kuwavula iwo; kunja uko mu maofesi, ndi kumayendetsa magalimoto a takisi, ndipo kukwera-ndi-kutsika ndi msewu. Kumene, iwo akuyenera kukhala ali kunyumba, kuseri kwa chitofu, akuphika, ndi kukonza zakudya.

¹⁸⁵ Ndi chiyani icho? Ndi Mdierekezi. Kuwukiridwa kukuchitika. Ine sindikunena kanthu zokhudza *uyu* payekha kapena *uyo* payekha. Ine ndikunena kuti ndi mizimu yoyipa imene ikuwagwira anthu, kuwayendetsa iwo kumene kupita mu izo. Kuwukiridwa kwa United States!

¹⁸⁶ Kulandidwa kwa mpingo! Mpingo walandidwa ndi Mdierekezi. Mmbuyo kutali. . .

¹⁸⁷ Iwo amamutenga mnyamata tsopano, pamene iye afika ku seminare, chinthu choyamba chimene iye ayenera kuphunzira ndi kutenga madigirii ake. Iye ayenera kutenga kuwerenga maganizo. Iye ayenera kutenga zamulungu. Iye ayenera kuphunzitsa, kutenga mtundu wonse wa zinthu kuphunzitsidwa mwa iye. Ngati iye alibe maphunziro abwino kwenikweni, ngati iye sali wanzero ndi wochangamuka momwe iye angakhoze kukhalira, ndiye iwo amukana iye; iye sangakhoze kupambana. Kodi iye angachite chiyani? Kutu, apite kunja kuno ndi kukapereka kuyankhula pang'ono mwandale, monga izo zinaliri, kuyankhula mwandale kwa mpingo, kwa gulu la anthu, gulu la amuna ndi akazi amene akufa.

¹⁸⁸ O Mulungu, mutitumizire ife kachitidwe kachikale kena, amuna olalikira achikale achimidzi amene samadziwa A kwa B, amene amadziwa Mphamvu ya chiwukitsiro cha Ambuye Yesu Khristu, amene ati adzalalikire kulapa, ndi kutumiza amuna ndi akazi ku guwa, kuti azikonda Ambuye Yesu. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

¹⁸⁹ Ndicho chobwerekera. Iye wawukira maseminare. Iye wawukira mipingo. Iye wawavula akazi athu. Iye watengera

amuna athu kupita ku malo amene iwe sungakhoze kuwauza iwo kanthu. Ndipo amuna ndi akazi, ine ndikuganiza . . .

¹⁹⁰ Inu mukuti, “Chabwino, akazi!” Inde, ndipo inu amuna amene muti muwalole akazi anu kuti azichita zimenezo, izo zikusonyeza chimene inu mwapangidwa nacho. Ndizo chimodzimidzi basi. Ndithudi. Ndi chamanyazi. Ndi chachisoni.

¹⁹¹ Ndiyeno mpaka kwa mlaliki. Mlaliki amayima mu nsanja, lero, la makono gu- . . . guwa. Kuyima mmenemo, ndi anthu ake patsogolo pake, ndi kulalikira za kanthu kalikonse kakale mu dziko pambali pa kulapa ndi tchimo, ndi mtanda wachikale wa Khristu. Inde.

¹⁹² Pamene iwe uyala zoonza pansu; anthu amabwera kudzakumvetsera iwe, mu msonkhano wa ulaliki. Iwe ukuyesera kutenga chinthucho ndi kulalikira Uthenga, ndi kuwatengera anthu ku kulapa ndi kuwachotsamo iwo; iwo amafufuma ndi kutuluka panja, iwo, “Sasowa kumvetsera Izo.” Ayi, iwo satero. Koma, abale, iwo adzayenera kuti alape kapena kuwonongeka.

¹⁹³ Ziwanda! Iwe ukapita ku sukulu; izo zawukira sukulu. Kuyang’ana pozungulira, mu dziko lero. Yang’anani kuno, anthu inu, inu Mprotestanti. Yang’anani, pali masukulu anai aakulu mopambana Achikatolika ndi zinthu, zomangidwa mpaka lero. Nchifukwa chiyani izo ziri? Inu mukulekerera zigwiriro.

¹⁹⁴ Palibe chotsutsa Chikatolika, ngakhale ine sindimakhulupirira mu icho. Ine ndine mosamalitsa Mprotestanti. Ndizo zolondola chimodzimidzi, ndipo ndikhoza kutsimikizira kuti iwo satero . . . Iwe sungakhoze kutsutsana nawo iwo. Iwo amati, “Ife sitisamala chimene Baibulo limanena. Ife timadziwa chimene mpingo umanena.”

¹⁹⁵ Mulungu ali mu Mawu Ake. [M’bale Branham agogoda pa guwa kasanu—Mkonzi.] Umu ndi mmene Mulungu ali.

¹⁹⁶ Koma ena a Chikatolika, akukakamira ku mpingo wawo, angakupange iwe kudzichitira manyazi wekha, ngati Mprotestanti. Ngati iwe ukanangomamatira kokha ku Baibulo, momwe iwo amamatirira ku mpingo! Ndiko kulondola. Koma, iwo akulakwitsa. Ine ndikhoza kunena izo pansu pa ulamuliro wa Mulungu Wamphamvuzonse, kuti, iwo akulakwitsa. Mwamtheradi.

¹⁹⁷ Ndipo inu Achiprotestanti mukulakwitsa, momwe inu mukuchitira, chifukwa inu mukudziwa bwinoko ndithu, ndipo inu mumachita zimenezo. Izo zimakupangani wachinyengo mwa inu. Zedi, ndiko kuwukiridwa; mipingo kulekerera pamenepo. Ndipo tsopano mmalo mwa . . .

¹⁹⁸ Mpingo, kuyesera kupanga tchalitchi chokongola, kumanga tchalitchi chachikulu, kuyika zichiri zazikulu pa icho, malimba aakulu kwambiri amipope, ndi kutenga chirichonse kuyesera kufanizira monga mpingo wa Katolika. [M’bale

Branham agogoda pa guwa nthawi zingapo—Mkonzi.] Inu simukufuna kufanizira monga mpingo wa Katolika, ngati iwo uli wotembereredwa kuti upite ku chiwonongeko. Pakuti, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE, iwo wotembereredwa kuti upite ku ziwonongeko. Ndipo ndinu chofanizira cha iwo, inu mukupita nawo iwo.

¹⁹⁹ Koma chimene ife tikusowa lero si mpingo wawukulu, chichiri chachikulu; ndi maguwa akachitidwe-kachikale pamene machimo akuwotchedwapo, pansi pa mapemphero a amuna ndi aakazi odzipereka amene amakonda Ambuye Yesu Khristu. Inu mukudziwa zimenezo. Ndicho chimene ife tikusowa. Ndimvereni ine, abwenzi. Ndimvereni ine. Ndicho chikondi.

²⁰⁰ Nthawi yanga yapita. Ine ndikungofuna kukhala pa izo, pamene...ine nditenga izo, kanthawi kenako, kuwukiridwa kumeneko, kumene iko kwapita. Iko kwawukira. Iko kwawukira mafuko athu. Iko kwawukira United States.

²⁰¹ Tsopano kumbukirani, ine sindinaponyepo voti mu moyo wanga; onani, ine ndinatero...kuti ndibwekererepo. Ndiwo mafulu anga akubadwa a Chimerika ngati ine ndikufuna kuchita izo. Koma ine ndimaganiza mochulukwa kwambiri za amzanga, kuti ndiwaike iwo mmenemo. Penyani, ine ndawaona iwo akulowamo ngati amuna abwino, akutulukamo ngati akuba, ndipo ine sindikufuna zimenezo.

²⁰² Ine ndiri ndi chinthu chimodzi. Ine ndiri pano kumangira nsanja Munthu mmodzi Amene ali woyenera, ndipo ndiye Yesu Khristu, ndipo Iye yekha. Ine ndikupereka nthawi yanga chifukwa cha Iye. Ndiko kulondola. Ngati ine ndingakhoze kuwutenga mpingo kuti uwongoke, dziko lonse lidzisamalira mwa lokha. Ndiko kulondola.

²⁰³ Koma ndiroleni ine ndikuwuzeni inu, pamene Bambo Roosevelt...Bamboyo anafa. Msiyeni iye apumule; ine ndikudalira iye ali. Anabweramo, ndipo anakhalamo katatu kapena kanai, ndipo anaposedwa, basi kuyambirira kwa kulamalira mwankhanza. Ine ndikhoza kutsimizikira kwa inu, kuti mu Lembu, kumene Izo anati zikanadzachitika. Ndiko kulondola. Ife tiribenso chi pepala cha malamulo. Ilo lasweka mwa zidutswa. Chirichonse chiri zonse zonyengezedwa. A Republican ali basi oyipa mofanana. Ndi sikisi kwa amodzi, theka la dazeni kwa amzakewo.

²⁰⁴ Pakuti, ufumu uliwonse uphwanyidwa, koma Ufumu wa Yesu Khristu udzayima ndi kulamalira kwa nthawizonse. Ndiko kulondola. Pamenepo...Daniele anawona Mwala wosemedwa kuchokera ku mapiri, ndipo unamenya dziko landale kumbuyo uko ndipo unaliswa ilo kukhala mungu woperedwa monga choncho, monga tirigu pa bwalo lopunthira mu nthawi ya chirimwe. Koma Mwala umenewo unakula

kukhala phiri lalikulu limene linatambalala pa miya... unadzazitsa miyamba yonse ndi dziko lapansi. Ndizo izo.

²⁰⁵ Dziko landale lapita. Fuko lathu lasweka. Inu muzikumbukira zimenezo, kuti M'bale Branham ananena kuti, PAKUTI ATERO AMBUYE. Fuko lathu layaluka. Ilo silidzawukanso. Ilo lapita, monga mafuko ena onse. Ilo ndi fuko lalikulu kwambiri mu dziko, layima lero, koma mbewu yomwe ya Mdierekezi yabzalidwa mu mitima ya anthu; momwe izo zinafikira mu Hollywood, momwe izo zinafikira mwa anthu, ndi kuyamba kwa izi. Ndipo inu simungakhoze kuwauza iwo kanthu.

²⁰⁶ Kumutengera Purezidenti kunjira uko yemwe ati ayese kutseka mowa, ndi kusakhala ndi kuletsa, muwone chimene chingachitike. Iye akhoza kuwomberedwa, mu maora awiri atati wafika mkati mmenemo. Zedi, iye sangakhoze kupirira zimenezo; dziko lonse liri kumutsutsa iye. Inde, bwana. Inu simukanakhoza kuchita izo.

²⁰⁷ Ilo lapita. Ilo lawukiridwa, ndipo mzimu wa chikominizimu walanda ilo.

²⁰⁸ Mupite ku masukulu athu lero, kawoneni pa ana athu asukulu. Anthu athu aang'ono amene amapita ku sukulu, iwe ukuyenera kudziwa basi chimene chimachitika. Asungwana aang'ono kumusi kuno mu masukulu, ndi zinthu ngati izo, pa usinkhu wa khumi ndi zinai ndi khumi ndi zisanu, mayi wawo anawatumiza iwo ku sukulu, owonongeka mwakhalidwe, mmalingaliro, ojayira chamba, ozolowera chamba, okhwewa ndudu, china chirichonse monga choncho; ndipo usinkhu wawung'ono kwambiri, ana aang'ono monga choncho. Chingakhale chovuta ngakhale kumupeza namwali pakati pa ena a iwo monga zikanakhalira kuti uipeze singano mu mulu wa nsipu, kumene iwo ali ndi ubwanawe wa m'bulangeti ndi anyamata, ndi kudziwongola pa magombe a mtsinje awa ndi kwina kulikonseko.

²⁰⁹ Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu, abwenzi anga. [M'bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ine sindikananena izo pa guwa ine ndikanapanda kudziwa zimene ine ndikuyankhula. Za masukulu komwe kuno mu zathu—zigawo zathu, komwe kuno mu zigawo izi, za mavalidwe a madona aang'ono awo, sali kudziwa... kumawauza amayi awo kuti iwo akupita ku malo osiyana, ndi kumakomana ndi anyamata ndipo ngakhale kumachita uhule pa misewu ya Louisville, (ndi chiyani icho?) ndi kumayimba mu makwaya.

²¹⁰ Chifukwa, iwo ali ndi Uthenga waung'ono umenewo wachitukuko ataima pamenepo, kumene alaliki amaima ndi kuyankhula zinthu pang'ono zachabechabe, ndi nthano zazing'onozing'ono za Baibulo kapena chinachake chonga icho,

mmalo molalikira kulapa ndi kuwabweretsa amuna ndi akazi ku guwa.

²¹¹ Abambo ake amalowa mnyumba usiku ndi kuyatsa ndudu yawo, kutenga chikho cha mowa, ndi kukhala pansu ndi kumamwa iwo. Mayi ali kunjwa, nthawi ya tsiku lonse, ndi gulu la akazi pa phwando lina la juga, zina zachitukuko ngati izo. Inu mungakhoze bwanji kuyembekezera mwanayo kukhala chinthu china chirichonse?

²¹² Penyani, chikhalidwe chirichonse chimene inu mumakhalamo, ndicho chimene inu muli.

²¹³ Inu mutenge msungwana wamng'ono kwambiri, mnyamata wamng'ono kwambiri, kuwaika iwo kuno, kuwalola iwo azikhala ndi winawake. Inu mumutenge mwamuna, ine ndikhoza kutenga mnyamata wanga, kumulola iye kukhala kunjwa kwa tsiku ndi winawake; mudirole ine ndibweremo, ine ndikhoza nthawizonse kukuuzani inu yemwe iye wakhala ali naye. Ndithudi. Penyani, chikhalidwe chimenecho, mzimu umenewo umamugwira iye.

²¹⁴ Inu mupite ku mpingo, kumene anthu onse...inu mukapita mu mipingo ya Mzimu Woyera, kapena mipingo ya Chipentekoste, iwo amayitcha iyo. Kulola aliyense kuti akhale...O, iwo amathamanga ndi kugwedezera mutu wawo mmbuyo ndi mtsogolo, m'busa akamatero; mupenye mpingo wonse uyamba kuchita chinthu chomwecho. Muwalole amuna, anthu, ayimirire ndi—ndi kumangopitiriza moyipa, kapena chinachake chimzake; mupenye chinthu chonsecho chikuchita izo. Kufika pa malo pamene m'busa ali wokhuthala kwenikweni ndi wozizira; mupenye gulu lonselo likuchita izo. Inu mwafika mu chikhalidwe chimenecho.

²¹⁵ Inu mumutenge mwamuna yemwe ali mwamuna wa khalidwe labwino, ndi kumulola iye kukwatira mkazi wamng'ono uyo yemwe sali wokwanira kobiri; sipatenga nthawi mpaka iye sakwaniranso kobiri nayenso. Ndicho chimene chinachitika kwa Ahabu. Tengani chomwecho, mosinthanitsa, mumulole mkazi wamng'ono wabwino akwatiwe ndi mwamuna wachikulire yemwe sali wokwanira kobiri; chinthu choyamba inu mukudziwa, iye akuchita chinthu chomwecho iye ali.

²¹⁶ Ine ndingakhoze kupita motani, mmawa uno, ndi kuloza manja anga pa khomo lophwasuka ndi zinthu monga izo, kumene mayi wamng'ono wokongola amabwera kwa bambo wolezera, ndi zinthu ngati izo, ndi kumaganiza kuti iwo angakhoze kuchita chinachake ndi iwo, ndipo tsopano mayi aliyense ndi onse a iwo akumwa ndi kumapitirira. Ndi malowo.

²¹⁷ Ndi chiyani icho? Ndi Mdierekezi. Ndi Mdierekezi, kuwukiridwa. Iye anasesa mu fuko ili, ngati mkango wobangula. Iye anadzikhazika yekha pansu pano mu malo abwino amene iwo anali nawo, mu Hollywood. Iye anati, "Ine ndikhoza

kutengera akanema kuno mpaka televizioni ibwerepo, ndiye ine ndiwatenga iwo.” Ndipo iye nkukhala pansi pamenepo.

²¹⁸ Ndipo anthu a mpingo, mmalo motseka ziwonetsero ndi kusawalola ana awo kuti apite, iwo amawapatsa iwo ma teni tambala Lamlungu madzulo ndi kuwatumiza iwo kumeneko, kotero kuti iwo akakhoze kukakhala ndi phwando lapang’ono la chitukukuko cha juga, kukhala kunja kwa okhaokha ndi kukakwera nakazungulira. O, ndi chamanyazi bwanji! Tsopano iwo amangotsegula televizioni ndi kuwonera uve wonse, kuyankhula kwamkhutu kovunda kumene kulipo mu dziko, pa iyo. Ndiko kulondola.

²¹⁹ Ine ndiribe kanthu kotsutsa kanema. Ine ndiribe kanthu kotsutsa televizioni. Ndi chinthu chovunda chimene chiri pa iyo. Ndicho chimene icho chiri. Ngati inu mukadaisunga iyo mwakhalidwe, iyo ikanakhala ya zamakhalidwe.

²²⁰ Inu sibwenzi mukugulitsa mabatani a nsapato a kachitidwe-kachikale kuno mtawoni, lero, nkomwe. Akazi sawafuna iwo. Iwo akufuna zala zawo zizituluka mwa izo. Akazi onse akuchita zimenezo. Ndiko kulondola.

²²¹ Pamene iwe upita ku tchalitchi, iwe sungakhoze kuwagulitsa iwo chipembedzo cha nthawi-yakale, chifukwa, mkazi wina, iye sakufuna kanthu kochita nazo izo. Ayi, bwana. “Ndipo palibe kusoweka ine kumapita kumeneko. Ine ndikungokhulupirira, ndizo zonse zimene ziripo kwa izo.” O, m’bale, Mdierekezi amakhulupirira, nayenso. Ndiko kulondola. Inu mulapa kapena kuwonongeka.

²²² Tsopano, pepani; ayi, ine sindiri. Ayi, ine sindiri. Ayi, ine ndikubweza chimenecho. Ine ndimawakonda anthu. Koma ine—ine ndimakukondani inu mwabwino kochulukuka kuti ndizikuonani inu mukupita mukugwa cha dodolido monga choncho. Ngati Mulungu alola, ine ndidzazitenga izi kanthawi kena mu sabata.

²²³ Tsopano, kwa inu amai amene ali anakubala, mawu chabe kwa inu tisanapite. Mulungu akudalitseni inu. Inu muwalere ana anu molondola.

²²⁴ Ife tikutenga kuwukiridwa uku; ife tiyenera kupita mu makwathu, ndi malo osiyana, masukulu, ndi kunja mu malo ndi iko. Ife tikutenga iko.

²²⁵ Koma, kuwukiridwa kwa United States, Mdierekezi walilanda ilo. Musati muchite mantha ndi Russia. Russia alibe kanthu koti achite. Ife tikuchita izo ifeeni, kuvunda kwathu komwe pakati pathu pomwe. Ndiko kulondola

²²⁶ Inu mukudziwa, United States ali ndi milandu yambiri ya kulekana kuposa onse mu dziko lonse; kulekana kochulukuka. Taganiza za izo. Sindizo zoyipa? Umayi waswedwa kale. Amai

sakukhalanso pakhomo ndi ana awo, monga iwo ankachitira. Iwo ayenera kukhala pa ntchito.

227 Kuno tsiku lina, munthu wina wa golosale mu mzinda uno, anali kuyankhula kwa ine za izo. Akazi awa ogwira ntchito mu malo a anthu, akazi aang'ono okwatiwa awa okhala ndi gulu la ana aang'ono. Iwo ali ndi olera ana kumawasamalira ana awo. Iwo amagwira ntchito mu malo a anthu awa. Anati, "Apo panali awiri a iwo ataima pamenepo, . . . ? . . . amene anaimikidwa, ku ntchito zawo za malo a anthu, anati, 'Musati mudandaule. Ife tidzazikwanitsa izo, mulimonse.'"

228 O, ora lotero la uhule layandikira! Zedi. Mdierekezi wawauza kale iwo kuti ndiwo mabwana a mnyumba. Iwo apanga njira yawo yomwe. Iwo achita chimene iwo akukhumba kutero. Ndipo inu muichotse iyo kwa iwo, ngati inu mungathe.

229 Pali chinthu chimodzi chokha chingaichotse iyo kwa iwo, ndilo guwa, pamaso pa Yesu Khristu, chipembedzo cha kachitidwe kachikale, cha mtsinje wa misonzi chimene chidzaswe mitima yawo ndi kuwang'amba iwo ku zidutswa, ndi kuwapanga iwo chimene iwo akuyenera kukhala. Ndiko kulondola.

230 Iwo akhoza kuganiza kuti ine ndiri chabe munthu wachikulire wopusa. Koma tsiku limene iwe ukufa, m'bale wanga, mlongo, iwe udzazindikira kuti ine ndinkakuuza iwe Choonadi. Ndiko kulondola.

231 Iye ali pa, kuwukiridwa, ora liri pano. Tsopano, inde, ora la kusankha, nalonso, ora la kusankha; osati kuti uzibwera ku mpingo, koma ora la kusankha ngati iwe uti upite kuti uzikamatumikira Khristu kapena kukhala wofunda mu mpingo wanu. Ndipo ndiko kulondola.

232 Alipo mamembala ambiri a mpingo. Ngati onse mame- . . . kapena anthu a Amerika amene amadzinenera kukhala Akhristu, akanakhala Akhristu enieni, Akhristu obadwakiwiri, m'bale, ife tikanakhala otetezedwa momwe iwe ukanakhallira Kumwamba, pafupifupi. Vuto lachivundi, inde, bwana, matenda akanasiya dzikoli, china chirichonse.

233 Kodi icho sichikanakhala chabwino kubwera pansu mu msewu ndi kuwona kumene dona akubwera, ndipo mwamuna, "Muli bwanji, mlongo? Mmawa wabwino, m'bale"? Kuyenda pansu, apo palibe. . . Iwe ulibe kudandaula kumodzi mu dziko. Chirichonse chiri chabwino basi ndi chokoma. Ndipo mnyamata akamabwera ku ngodya ya msewu; mmalo moyesera kuti akugunde iwe, iye nkuyima, "Chabwino, m'bale. Chabwino, inu munali. . . O, inu patzogolo pa ine," inu mukuona, kungololera. . . Kodi icho sichingakhale chodabwitsa? [Osonkhana anena, "Ameni."—Mkonzi.] Ife tikakhala nacho icho, koma ndimo mu Zakachikwi, m'bale. Tsiku likubwera kumene. Ndiko kulondola. Koteru tsopano ife sitiri. . .

²³⁴ Ine ndinaima kwa oyandikana nawo athu, kuno tsiku lina; palibe chotsutsa oyandikana nawo athu, koma ine ndikhoza kuzindikira ana athu aang’ono. Mkazi wanga anali kulira. Dokotala wina wa mzinda uno, msungwana wake wamng’ono anali kuyendayenda ndi msungwana wanga wamng’ono, ndipo iwo anakondana wina ndi mzake; mpaka iwo anadzapeza kuti dzina lake linali Branham, ndipo iye anali mwana wa M’busa Branham. Izo zinakhazikitsa icho. Msungwana wamng’onooyo sakanakhoza kumayendanso ndi msungwana wanga wamng’ono. “Mai,” ine ndinaganiza, “chabwino, zabwino.”

²³⁵ Ena a oyandikana nawo aang’ono anathamangira kumeneko, anati, “Chabwino, izo zinali zabwino.” Kotero, iwo anapita kwa abusa awo. Musati mundiuze ine. Inu mukudziwa, ine—ine ndiri nayo njira yodziwira zinthu zambiri, inu mukuona. Kotero iwo—iwo anapita kwa abusa awo, ndipo anati, “Inu mukudziwa, pali mwamuna yemwe amakhala moyandikana nawo kwathu, iye ndi wabwino kwambiri kwa ana athu.” Anati, “Ndi M’busa Branham. Iye amawatenga iwo, kuwakokera iwo mu galimoto yake yaying’ono yakale, ndi kuwatengera iwo kunja.”

²³⁶ Anati, “Chabwino,” [M’bale Branham ayeretisa kummero kwache—Mkonzi.] “ife tiribe kanthu kotsutsa M’busa Branham. Iye ndi wabwino, koma, inu mukuona, iye ali chabe kalasi yosiyana ya anthu kusiyana ndi imene ife tiri.” Mukuona? “Ife tiri, ine—ine ndikanati kuti inu mukanakhala kuti simuli . . . inu mukudziwa, ine sindikanakhala ngati . . . Inu muziyankhula kwa iwo, ndi kukhala mwaubwenzi, koma mulole basi awo akhale mapeto.”

²³⁷ O, m’bale! Mkazi wanga anali kuima pamenepo, akulira. Ine ndinati, “Wokomamtima, ndiwo mzere wolekanitsa. Koma kwa ine ndi nyumba yanga, ife tidzatumikira Ambuye.”

²³⁸ Ngakhale dziko lonse lichoke; komabe Yesu Khristu! Ngati ine ndingatchedwe wotentheka, ngati ine ndingamati ndizikanidwa ndi achibale anga, munthu mzanga, ndi zinthu ngati zimenezo, ine ndikusankhabe Yesu Khristu. Kugwiritsa ku dzanja la Mulungu losasintha. Pamene amzanu a dziko lapansi akukanani inu, komabe pafupi kwambiri kwa Iye kangamirani. Gwirani kwa Iye.

²³⁹ Mulungu, mudirole ine ndilalikire monga ine sindinateropo kale. Mudirole ine ndilalikire kwa anthu akufa, ngati munthu wakufa, inemwini. Mudirole ine ndilalikire kwa anthu ngati kuti ine sindidzakhalanso ndi ulaliki wina woti ndilalikire. Mudirole ine ndiwakakamizire iwo kuti abwere ku guwa, ndi nkhope zokuwa, ndi nsozi; kubwerera kunyumba ndi kukhala moyo ngati Akhristu, ndi kukhala ndi oyandikana nawo. Kusiya zonse izi pano zodyerekeza ndi kumathamangathamanga kuzungulira, ndi kudumphu ndi kumapitirira; ndi kumachita

mwa njira *iyi*, ndi kumafufuma pa *izi*, ndi kumapita njira *iyi*. O, musati muzichita zimenezo. Ameneyo ndi Mdierekezi. Mizimu imeneyo ya ziwanda itabwera pa Akhristu.

²⁴⁰ Kumbukirani, atumiki aja kumusi uko, iwo anali aneneri aja. Iwo anali aneneri. Iwo anali amuna achipembedzo akupereka nsembe. Iwo anali achipembedzo basi monga aphunzitsi a tsiku lino, koma, m'bale, iwo anali njira zakutali kwa kudziwa choonadi.

²⁴¹ Kodi inu simukuona momwe Mdierekezi aliri wachipembedzo? Mdierekezi sali ayi wotsutsa-, chinthu chachikulu monga chikominisi, zonse zotsutsa Chikhristu. Sindizo ayi. Ndizo basi zonse za Mdierekezi, zedi, koma sindiye wotsutsakhristu. Wotsutsakhristu ndi wachipembedzo kwambiri, wachipembedzo kwambiri. Iwo unali mzimu wachipembedzo umene unamupachika Yesu. Ilo nthawizonse lakhala dziko lachipembedzo, anthu achipembedzo, amene amapachika. Ndi anthu achipembedzo amene anali otsutsa Khristu woona. Iwo anali aneneri achipembedzo amene anali kumutsutsa Mikaya. Ndi anthu achipembedzo a tsikuli amene akutsutsa Uthenga wa Mulungu.

²⁴² Kumbukirani, ine ndakuchenjezani inu. Ine ndakuuzani inu. Ine sindiri kuyankhula mochuluka kwambiri za Chikatolika, ndi Chibaptisti ndi Chimethodisti; ine ndikungoyankhula za anthu omwe ali anthu achiyero, mpaka pansi mizere iyi pano. Kuyang'ana pa izo lero, momwe izo zabwerera ndi kumaima mu seweru. O, mai! Ine ndikapita mu izo, nthawiyina. Ndipo mtima wanga umasweka mkati mwa ine.

²⁴³ Ataima pamenepo ndi banjo yachikale, kumakhwacha banjo yachikaleyo, ndi kumaliza chitoliro chakale monga choncho, "Kodi uyu ndi mnyamata wolishya ng'ombe wa ku Texas *Wakuti-ndi-wakuti*?" Ine ndiribe kanthu kotsutsa munthuyo; koma izo ziri za kunja uko mu dziko kunja uko. Ndiko kulondola. Ine kulibwino ndiyime, m'bale, wopanda ngakhale kanthu, ndipo osadziwa kanthu nkomwe, koma kungoima ndi kukweza manja anga ndi kunena, "Yesu, mundisunge ine pafupi ndi mtanda." Inde, bwana.

Mtanda wopatulika ine ndidzaunyamula,
Mpaka imfa idzandimasule ine,
Ndiye nkupita Kwathu, kukavala korona,
Pakuti kuli korona wa ine.

²⁴⁴ Kwa inu amai aang'ono kuno mmawa uno, amene mwakhala amai enieni, ndipo ine ndikudziwa mulipo ambiri a inu; ine ndikuganiza, mmodzi aliyense wa inu. Mundirole ine ndikuuzeni inu chinachake. Mulungu akudalitseni inu. Ndinu Uthenga wachisanu, ine ndikuganiza. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chiyani tsopano chifukwa cha ana anu, kanthu kakang'ono chabe. Chifukwa, M'bale Neville mwinamwake adzalalikira

pa . . . zokhudza anakubala usikuuno, kapena aliyense, mmodzi wa ife amene akulalikira, chabwino, zokhudza anakubala. Koma, mvetserani, ndiroleni ine ndikufunsemi inu chinachake.

²⁴⁵ Kumbukirani, pamene Mose anali mnyamata wamng'ono, anali mayi amene anamupatsa iye malangizo ake. Iye anali mayi waumulungu amene anamunyamula Mose wamng'ono pa maondo ake, ndipo anati, "Mose," anamuphunzitsa iye zonse. Iye anali mphunzitsi wake kapena . . . Iye anali mphunzitsi wake, kani, pansu pa Farao, ndipo anati tsopano zinthu izi. Anati, "Mose, tsiku lina iwe udzawawombola ana a Israeli. Ndiwe mnyamata amene waitanidwa. Dzisunge wekha mwangwiro ndi mopanda banga kwa dziko, pakuti ndi iweyo. Ndi iweyo."

²⁴⁶ Palibe malo ena amene ife tikuwadziwa, amene iye anayamba wapitako ku seminare iliyonse, kuphunzitsa kulikonse nkomwe, iye anakhala nako konse. Iye anakhala kumene mu nyumba yachifumu ya Farao, yemwe anali wachikunja; koma mayi ake ankamuphunzitsa iye. [M'bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ameneyo ndi mayi weniweni. Iye anamuphunzitsa iye malangizo a Ambuye. Iye anamuza iye momwe iye ayenera kukhala woyera. Iye anamuza iye momwe iye ayenera kukhalira moyo, ndi momwe, chimene Mulungu ayenera kuchita, akanati adzamuchitire iye. Ndipo izo zinakanirira kwa Mose masiku onse a moyo wake.

²⁴⁷ Ndipo mayi aliyense wabwino, wona, womvera yemwe angatenge ana ake aang'ono, mmalo mowatumiza iwo ku ziwonetsero za zithunzi ndi madansi, ndi zina zotero monga choncho, ndipo iye nkuwaika iwo pa chilolo chake ndi kuwaphunzitsa iwo za Ambuye Yesu Khristu!

²⁴⁸ Kuno tsiku lina, ine ndinali kuyankhula kwa mayi pa telefoni. Ndipo mayiyo anati, "O, M'bale Billy," iye anati, "mnyamata wanga wosauka ali mu vuto." Ainati, "O, ndi vuto bwanji limene iye alimo!"

²⁴⁹ Ine ndinati, "Inde, ine ndikudziwa za izo, mlongo, wokonedwa." Ndipo iye anati, "Iye akhoza kukhala atalakwitsa. Ine sindikudziwa." Anati, "Wina akunena *izi* ndipo wina akunena *izo*. Ine sindikudziwa. Koma," anati, "ziribe kanthu kaya iye akulakwitsa kapena akulondola, ine ndimamukonda iye." Ndi zimenezotu, "Ine ndimamukonda iye."

²⁵⁰ Iye anati kwa mayi ake, anati, "Ine ndanyengedwa kwambiri ndi *izi* ndi *izo*." Anati, "Mayi, ine ndikukhulupirira ndinu pafupi wokomamtima yekhayo yemwe ine ndiri naye kwenikweni; mkazi yemwe ali wona kwa ine, ndi kumamatira kwa ine." Ndicho chikondi cha mayi. Ndiye mayi weniweni yemwe ati ayike mikono yake mokumbatira mwana wake. Mosasamala kaya iye akulondola kapena akulakwitsa, iye nkupitabe kwa iye. Ndipo ngati Mulungu . . . Ngati mayi angakhoze kuganiza

izo za mwana wake, ndi mochuluka bwanji momwe Mulungu amaganizira izo za Wake! Inu mukuona? Inu mukhale naye kumene Iye. Pitani molondola.

²⁵¹ Ndipo tsopano mudirole ine ndingokuuzani inu mayi wina, mofulumira ndithu, mu Baibulo, ife tisanatseke. Panali mayi wotchedwa Herodia. Iye anamuphuzitsa mwana wake wamkazi kuvina kwasakwa. Iye ankafuna iye kuti akhale wotchuka. Ndipo iye anavina pamaso pa mfumu, ndipo anafunsa mutu wa Yohane M'batizi. Ife tiri nawo umboni wa makumi asanu ndi awiri a mphukira zake, buthu ili limene linavina pamaso. . . Mwana wamkazi wa Herodia anavina pamaso pa Herode; makumi asanu ndi awiri a mphukira zake, iwo mwina anafa ali mahule kapena pa zokoloweka.

²⁵² Mayi mmodzi anaphuzitsa wake zinthu za mdziko; mayi winayo anaphuzitsa wake zinthu za Mulungu. Wina anakhala mtsogoleri wamkulu ndi mgonjetsi, wachisavundi pakati pa anthu lero; ndipo winayo woipitsidwa ndipo ali mu gehena, ndipo watenga zikwi kuphatikiza zikwi ndi iye. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? “Mulereni mwana mwa njira imene iye ayenera kupita nayo.”

²⁵³ Ndipo ine ndithudi ndikumva nanu inu chisoni amai osawuka mwakhala pano mutavala maduwa anu oyera. Kulipo Kumwamba kumene mayi wapitako, lero, kumene mayi wakachitidwe-kachikale amene anakhalira moyo Mulungu, mwinamwake wadutsa kupyola chotchinga. Iye akukuyembekezerani inu kuti mubwere. Ndiko kulondola.

²⁵⁴ Ine ndikukulemekezani ndi kukupatsani inu ulemu pamene muwale duwa lanu lofiira. Mayi anu, ngati inu mukufuna kuwachitira chirichonse iwo, muzichita icho masiku mazana atatu makumi asanu ndi amodzi mphambu azisanu pa chaka. Muzipita kunyumba yawo ndi kukapereka pemphero, ndi kukhalira moyo Mulungu. Ndicho chinthu choti uzichita. Ndi kuwalera ana anu. Ndipo pamene ana anu akula, iwo adzakutchani iwo “wodala,” inu mutadutsa kale kumka kuseri kwa chophimba. Ndiwo mzimu weniweni wa umayi, mzimu weniweni wa tsiku la anakubala. Tsiku la Anakubala ndi masiku mazana atatu makumi asanu ndi amodzi ndi mphambu zisanu pa chaka.

²⁵⁵ Ili ndi tsiku limene amagulitsa maluwa ndi kupatsana mphatso. Dziko limachita zimenezo. Ngati ilo lidutsa, ngati dziko litaima zaka zina makumi awiri, iwo adzakhala ndi masiku a mwana wamwamuna, ndi masiku a mwana wamkazi, ndi, kapena masiku a asuwani, ndi masiku a amalume, ndi zinthu zonse izo monga chomwecho, basi zokwanira kulitengera dziko mu kukongoletsa kwa malonda. Ndi basi kumene ilo likupita, ku gehena kumene, molimba basi momwe ilo lingathe kupitira, ku chiwonongeko.

Koma, inu, Mulungu akudalitseni inu, ndilo pemphero langa. Tiyeni tipemphere.

²⁵⁶ Atate athu achifundo Akumwamba, pamene ife tikuyang'ana mmbuyo, mmawa uno, ndi maganizo athu, kale kutali, mazana ena a zaka kale, pamene uko kunaima Yehosafati ataima pamenepo pambali ya Mfumu Ahabu. Ndipo mzimu wawung'ono pansu mu mtima mwake, utatsalirabe wa Mulungu, ngakhale iye anali atapanga kulakwitsa, anamuuzza iye, anati, "Uku ndi kulakwitsa. Uku ndi kulakwitsa. Izo si zoyera. Izo si zopatulika. Mneneri wanena kuti zinthu izi sizingakhoze kumapitirira monga chonchi." Ndipo Moto wawung'ono wa Mulungu unamudzutsa iye.

²⁵⁷ Ndiyeno Inu munali ndi winawake kuti ayankhe Moto waung'ono umenewo, amene anali Mikaya, mneneri woona wa Mulungu. Ngakhale kuti iye mwina anabwera pamenepo atavala mu zisanza, ngakhale mwina iye akanakhoza kubwera pamenepo wonyozedwa, ndipo onse awo akuyang'ana pa iye monga ngati gulu la ankhandwe akuyang'ana pa mwanawankhosa. Koma iye anawauza choonadi, ngakhale kuti iye anachita kukanthidwa pa nkhope, ngakhale iye anachita kuponyedwa mu ndende ndi kudyetsedwa mkate ndi madzi achisoni. Koma, apobe, mawu amene iye ananena anabwera pochitika, pakuti Inu munali ndi iye.

²⁵⁸ Mulungu, perekani, lero, ndipo ife tikuyang'ana pansu mu Baibulo ili. Ife tikuyang'ana pa mabuku a mpingo, nkhani khumi, ndi zina zotero, za mipingo, mipingo, ndi kuwona momwe iwo amachitira *izi, izo*, kapena *zimzake*. Koma mutilole ife tiyang'ane mu Mawu owona awa pano, ndi kuwona chimene Iwo ananena. "Popanda chiyero, palibe munthu ati adzawawone Ambuye. Tsatani mtendere ndi chiyero, chimene, popanda, palibe munthu ati adzawawone Ambuye. Iye amene akonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa iye."

²⁵⁹ "Mu masiku otsiriza nthawi zowopsya zidzadza. Anthu adzakhala odzikonda iwo eni, onyada, odzitamandira." O, zinthu zazikulu izo, Ambuye, zimene zikuchitika! "Ammutu, odzikweza, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu; kumawaphunzitsa anthu malangizo a—a anthu mmalo mwa malamulo a Mulungu; kukhala nawo mawonekedwe amulungu, ndi kumakana Mphamvu ya Mzimu Woyera" kuti umupange munthu kuti adzazidwe ndi Mzimu, kuti umupange iye kusangalala, kuti apangitse misonzi kuyenderera kuchokera mmaso ake, kuti umupange iye kutuluka kunja ndi kukapempherera odwala, kuti amupangitse iye kuyankhula ndi malirime ndi kutanthauzira, kuti amupangitse iye kulosera. Mzimu wa Mulungu, Mulungu wamoyo, iwo amangowuchotsapo Iwo kupita ku mphanga yina kapena chinachake chonga icho,

“Okhala nawo mawonekedwe a umulungu, ndi kumakana Mphamvu yake.”

²⁶⁰ O Mulungu, mulole omvera apang’ono awa, pa tsiku lino, agalamuke mwamsanga, pakali pano, nthawi yotsiriza isanafike, ndi kuchigwira icho mu chikhalidwe ichi. Mulole ife tikhale, kudzipanga tokha mwatsopano, monga Baibulo linanena, “Ukani ndi kudzigwedeza nokha. Ndi kufunsa njira yakale, imene ili njira yabwino; ndipo pamene inu muipeza iyo, yendani mu iyo.” Mulungu, perekani kuti ife tikhoze kupeza njira yakale yonyozeka, pamene ife tingakhoze kuima pamodzi kachiwiri, ngati mazana, ndi kulumikiza manja athu limodzi ndi kuimba.

Ine nditenga njira ndi onyozeka pang’ono a
Ambuye.

Ine ndayambamo ndi Yesu, ndipo ine ndikupita
mopyola.

Mulungu, tithandizeni ife kuti tikhale moyo chimenecho ndi kukhala chimenecho!

²⁶¹ Dalitsani amai okondedwa onse awa akhala pano, Ambuye; podziwa kuti iwo ndi amai, iwoeni, ali ndi maluwa oyera atamangidwa pa zikhoto zawo, mmawa uno, ngati chikumbutso cha mayi wakale wokondedwa yemwe wadutsa kuseri kwa powonekera. O Mbuye wa Moyo, adalitseni iwo, Ambuye. Ndipo mulole iwo adalitsidwe, nawonso, ndipo mulole zokumbukira za ana awo zikhale monga zawo ziri ndi mayi awo, ngati iwo apita kuseri kwa chotchinga, Kumwamba kwaulemerero. Perekani izo, Ambuye.


²⁶² Ndipo mmawa wina pamene moyo ukutsekeka kwa mitsempha yathu, ndipo kupuma kwathu kukulephera kubwera kwa ife, chotchinga chidzatsegukire mmbuyo; iye adzabwera pansu, mwinamwake, pa mapeto a Yordani, kudzatithandiza ife kuwoloka. O, ku tsiku laulemerero ilo pamene ife tidzaponda phazi lathu kutsidyako, kumene uko sikudzakhala. . . Mpweya siwudzayipitsidwa ndi utsi wa ndudu. Uko sikudzakhala woledzera pa msewu. Uko sikudzakhala hule. Uko sikudzakhala tchimo. Uko sikudzakhala kanthu konga kameneko. Koma, mwaulemerero kwanthawizonse, tidzakhala moyo ndi mtendere ndi Ambuye wathu Yesu Khristu ndi ana athu. Ndipo, o, ndi tsiku lodabwitsa bwanji!

²⁶³ O Atate, pamene mdima waukulu ulipo, nkhondo, ndi Mdierekezi zikuwukira maiko, ndi kuwukira maguwa, kuwukira mipingo, kuwukira anthu, kuwukira malonda, kuwukira mizinda, ndi masukulu ndi makomo; O Mulungu, tithandizeni ife kuyima, kusolola lupanga mwamsanga ndi kumenyera Mulungu, monga Mose ndi—ndi Alevi anachitira kumusi kuja pamene tchimo linali mu msasa. Tithandizeni ife, Ambuye.

²⁶⁴ Mutikhululukire ife tsopano, ndipo tidalitseni ife. Ndipo tisungeni ife odzichepetsa, tisweni ife, Ambuye. O Mulungu, Inu munati, “Iye amene apita, akubzala mwa misonzi, mosakaika adzabwereranso, akusangalala, akubweretsa limodzi naye mitolo.” O Mulungu, tisweni ife ku zidutswa. Tiwumbeni ife, mwatsopano, Ambuye. Ife tikupeza zochuluka kwambiri zosiya njira.

²⁶⁵ Ine ndiri, inemwini, Ambuye, ine ndikufika pa malo amene ine ndikuganiza za kuchuluka kwa amene ati adzakhalepo pa msonkhano wanga. O Mulungu, ine ndikufuna Inu muzikhalapo. Bwerani, Ambuye! O Khristu, bwerani Ambuye! Ndisweni ine; ndiwumbeninsu ine. O Ambuye, musati, musandirole ine kutengera zinthu zimenezo pa malingaliro anga. Mulungu, zisungeni izo kutali kwa ine!

²⁶⁶ Ndithandizeni ine, Ambuye, kuti ndizilalikira, monga ine ndinanena, kanthawi kapitako, ngati munthu wakufa kwa anthu akufa, podziwa kuti ife tonse tiyenera kukomana nawo Umuyaya. Ife tiyenera kuyima pamaso pa Inu; pamene Inu simuli mu chikhalidwe Chanu chokondweretsa, pamene Inu simuli ndi chifundo, pamene Inu mukuima wopanda chifundo; pamene Inu mukuima, wokwiya, kuti mubweretse chiweruzo pa mafuko ndi anthu amene akana ndi kukankha chikondi cha mwana Wanu.

²⁶⁷ Mulungu, tipatseni ife chifundo ndi Iye lero, kuti mu Tsiku limenelo ine ndikhoza kuima wotsimikizidwa. Ndisowa kulira tsopano, koma Inu mudzakupukuta iko kukuchotsa, ku chimwemwe, pa nthawiyo, pamene Inu mudzati, “Lowani mu zisangalalo za Ambuye, zimene zakonzeredwera inu kuchokera ku maziko a dziko.” Mulungu, khalani ndi ife tsopano, ndipo tithandizeni ife, ife tikupemphera mu Dzina la Yesu. Amenii. 

KUWUKIRIDWA KWA UNITED STATES CHA54-0509
(The Invasion Of The United States)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Mei 9, 1954, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1995 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1995 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org